

File Copy

Olemba Ndi Betty Morris



**ZIPHUNZITSO ZACIKHULUPIRIRO
NDI CILIMBITSO**

Teaching of Faith and Courage
Published March 1st, 1989
By Baptist Publishing House
P.O. Box 31995, Lusaka, Zambia

Designed By J.W.Tembo

Olemba Ndi Betty Morris



**ZIPHUNZITSO ZACIKHULUPIRIRO
NDI CILIMBITSO**

Designed By J.W.Tembo

**ZIPHUNZITSO ZA CIKHULUPIRIRO NDI
CILIMBITSO**

Printed by
Baptist Printing Ministry
P.O. Box 31995
Lusaka, Zambia

Copy Right March 1, 1989 All Rights Reserved

Published With permission of
International Publishing Services

By the Baptist Publishing House
P.O. Box 31995
Lusaka, Zambia

MUTU**TSAMBA**

1. Kodi Ndi Motani Momwe Munthu Adziwira Mulungu?	5
2. Yesu, Wansembe Wathu	11
3. Yesu, Pangano Latsopano	17
4. Cikhulupiro, Colimba Ndipo Coona	24
5. Umoyo Wa Cigonjetso	31
6. Ulemerero Wa Mulungu Mu cilengedwe	37
7. Munthu Ayang'ana Pa Cilengedwe Ca Mulungu	43
8. Pangano La Mulungu Ndi Munthu	49
9. Cikondi Ca Mulungu	55
10. Maonekedwe a Mulungu Ndi Munthu	62
11. Malamulo A Kukhala Umoyo Wabwino	68
12. Nchito Ya Munthu Aliyense	75
13. Ziopyezo Za Ucinjilidzo Wabodza	81

MUTU 1

KODI NDI MOTANI MOMWE MUNTHU ADZIWIRA MULUNGU?

COLINGA: Kuphunzira phunziro ili idzandithandiza kumvetsetsa kuti ndi khoza kudziwa Mulungu kupyolera mwa Yesu Kristu, Mwana wace.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Ahebri 1:1-2:9

NDIME ZA MPHUNZIRO YA LERO:

MAU APAMTIMA: *"Kulibe munthu anaona Mulungu nthawi zonse; Mwana wobadwa yekha wa kukhala pa cifukwa ca Atate, Iyeyu anafotokozera."* (Yohane 1:18)

"Ndimdziwa Yohane" anatero Samueli, Kodi titanthauza ciani pamene tinena kuti tidziwa wina? Kodi titanthauza kumuzindikira pamene timuona? Kapena titanthauza zambiri kupambana apa? Tikhoza kutanthauza kuti tidziwa zimene amacita, timvetsetsa colinga ca moyo wace, ndipo tidziwa zomwe aganzizira.

Kodi tikhoza kudziwa wina ngati tingolembelana makalata? Kodi tikhoza kudziwa bwino munthu pa kulankhulana naye pa lamyapa? Kodi anthu awa tiwadziwadi? Ai osati kokwanira. Tidzadzziwa zina za iwo, koma sitidzawadziwa bwino pokhapo titakomana nao maso ndi maso ndi kukhala nao.

Kodi Mulungu mumdziwa? Ngati nditero mumdziwa motani? Kodi mumdziwa monga bwenzi? Phunziro lathu la lero idzatithandiza kudziwa Mulungu.

BUKU LA AHEBRI:

Mlembi wa buku la Ahebri sadziwika. Iye ngakhale tero anaonetsa colinga cace poyera kuti owerenga amvetsetse. Colinga cace cinali kuthandiza Akristu a Ciyuda kukhala okhulupirika kwa Mulungu. Anaonetsa Akristu kuti Mulungu anazibvumbulutsira iye yekha mokwanira kupyolera mwa Mwana wace, Yesu.

Mlembi anafotokoza kuti, Yesu anali ndipo akali wopambana angelo, aneneri ndi anthu. Iye anafuna Akristu nthawi zonse kukhala okhulupirika kwa Mulungu. Anadziwa kuti Akristu akadziwa Yesu, adzadzizanso Mulungu ndi kukhala okhulupirika.

Kodi munthu amadziwa bwanji Mulungu? Kuli njira zambiri. Dziko lace lomwe tikhalamo litiuza za Mulungu. Mulungu analenga munthu mucifaniziro cace. (Genesis 1:26) Ndipo Mulungu anaitana munthu kumutumikira iye. Anafuna kuti amukonde ndi kumudziwa iye. Conco anawauza za iye.

Wina amasulire ndime zocokera mu Yeremiya. Mukhoza kuonjezera mau omwe acokera mu maphunziro oyamba. Pitolizani ndi izi kufikira mwazindikira kuti ophunzira amvetsetsa cifukwa comwe Yeremiya anali kucenjeza anthu.

Werengani Yesaya 31:1-3. Nenani: "Ndime izi zitiuza za malingaliro a Mulungu pa mtundu wa ci Yuda pamene anatumiza anthu kukapempha thandizo kwa Aigupto. "Uzani wina kuwerenga Yesaya 30:1-7. Nenani: Ndime izi zinena za nchito imodzi-modzi. Mulungu anadabwa cifukwa cace anthu anafuna kuika cikhulupiriro cao mwa mphamvu za Aigupto, pamene mphamvu ya Mulungu inalipo."

Nenani: "Mu Mika 6:6-8, Muli olankhula awiri, anthu ndiponso Mulungu. Ndifuna munthu m'modzi kuwerenga ndime 6 ndi 7 omwe ali mau a anthu, ndipo wina awerenga ndime 8 omwe ali mau a Mulungu."

Pamene atatha kuwerenga, nenani: "Anthu anadziwa kuti Mulungu sadzafuna nsembe zazikulu kwa iwo. Mulungu sanakondwera ndi kuyelekeza kwa kumvera kwa iwo. Mulungu anadziwa mitima yao. Anadziwa kuti anali anthu ocimwa, omwe anali kugwiritsa nchito zipembedzo ngati zicinjirizo mu dziko. Mulungu anawauza kuti comwe anafuna kwa iwo cinali kuyera mu miyoyo yao."

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU:

Nenani: "Mulungu afuna cimodzi-modzi kwa ife ngati tiri Akristu. Afuna ife kuti tikhale umoyo olungama ndipo oyera, kukhala ndi anansi athu bwino, mu kukoma mtima ndi cikondi. Afuna ife kuti tikhale okhulupirika nthawi ili yonse kuti tiyende ndi Mulungu wathu. Afuna ici kwa ife tonse."

"Ngati inu sindinu Akristu, cinthu coyamba comwe Mulungu afuna kwa inu ndi kutembenuka ku macimo anu ndi kukhulupirira Kristu monga Mpulumutsi wanu. Ndipo mukhoza kumukhulupirira mu umoyo wanu wonse."

Nenani: "Mulungu afuna kuti ife tikhale ndi zinthu zabwino mu umoyo wathu: 'Nchito zabwino, nyumba, mabanja abwino, cakudya ca mabanja athu, maphunziro ndi zina'. Koma safuna kuti tizikhulupirire ndi kumuiwala iye. Iye afuna kuti tibweretse zonse kwa iye. Afuna kutithandiza ife. Ali okonzekera kukwaniritsa malonjezo ace mu umoyo wathu."

Funsani ngati pali mafunso pa phunziro lanu. Yankhani ngati mukhoza, kapena auzeni kuti mudzabweretsa yankho sabata lotsatira.

Tsekani ndi pemphero.

Ndime 8-15 inena kuti Mulungu ananena za zisanu za malamulo khumi. Kodi anthu anaganiza kuti adzaswa malamulo awa mu umoyo wao wamasiku onse, ndi kubwera kukacisi kukapembedza? Mulungu sakana landira cipembedzo coteri! Anthu akanapita ku Shiloh, ndi kuona zomwe zinacitika kumeneko. Ukunso kunali kumalo komwe Mulungu anakhala, koma kunaonongedwa. Mulungu analola izi kucitika cifukwa ca mayendedwe a anthu. Analonjeza kuti adzacita cimodzi-modzi ndi Yeresalemu zomwe anacita ku Shiloh.

Yesaya 31:1-3 afanana ndi mau omwe alipa Yesaya 30:1-7. Pamene Mulungu anazuzula mtundu wa ci Yuda cifukwa anaika cikhulupiriro cao mu mphamvu za Aigupto. Mulungu anafunsa cifukwa cace cimene anakhulupirira mphamvu imeneyi pamene mphamvu ya Mulungu inalipo.

Mika 6:6-8 ili ndi olankhula awiri. Anthu aci Yuda analankhula mu ndime ya 6 ndi 7. Mulungu anayankha mu ndime ya 8.

Anthu anafunsa Mulungu ngati iye sanali okondwa ndi nsembe zao. Iwo anacita zonse zimene akanakhoza kucita ndi kuganiza, kukundweretsa Mulungu. Nsembe zao zinaoneka ngati sidzinakwanire. Kodi Mulungu akanakhala okondwa ngati iwo akanaonjezera? Kodi Mulungu anafuna kuti anthu apereke ana ao munga nsembe?

Mulungu anayankha kuti anafuna anthu kucita izi mu njira yabwino, kukonda ndi kuyenda mozicepetsa ndi iye. Zinthu zomwe Mulungu anafuna kuti acite ndi kukhala omvera, ndi kukhala umoyo woyera. Zinthu zoonetsa zakunja zinalibe tanthauzo kwa Mulungu. Anafuna anthu kusiya njira zao za kale ndi kukhala mu ciyanjano ndi iye.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO ILI KUDZIWITSA:

Funsani "Kodi comwe cimapangitsa inu kumvera kapena kuganiza kuti muli ocinjirizidwa ndi ciani? Lembani mayankho awa pamene ali kuchulidwa. Iwo akhoza kunena kuti nchito yabwino, nyumba yabwino, mathupi anthanzi, ndalama zambiri. Ngati iwo anawerenga phunziro lao akhoza kunena "Mulungu yekha ndiye akhoza kupatsa ucinjilizo weni-weni."

Nenani: "Kodi ndi coona kuti Mulungu atipatsa ucinjirizo omwe tiri nao, koma timakhulupirira mu zinthu zambiri? Phunziro lathu lero ndi la ucinjirizo ndi comwe cinacitika pamene mtundu wa Ciyuda unaika cikhulupiriro cao mu zinthu zina."

KUMASULIRA:

Uzani ophunzira kutsegula ku Yeremiya 7:1-15, awerenge.

Uzani ophunzira wina kumasulira mbiri ya Ayuda yomwe inenedwa mu phunziro lao. Ngati ndi cotheka, ena anene zinthu zomwe mwaiwala kuchula.

MULUNGU ANALANKHULA KWA MUNTHU KUPYOLERA MWA ANENERI

Werengani Ahebri 1:1-4. Mulungu anafuna kulankhula kwa munthu. Anafunika anthu omwe anali kukonda Mulungu ndipo omvera. Anawaitana kumutumikira. Anawaitana mu njira zambiri.

Mulungu analankhula kwa Mose kupyolera mu citsamba ca moto. (Onani Eksodo 3:1-6.) Analankhula kwa Amose mu maso mphenya (Amose 1:1) Analankhula kwa Yesaya mu kacisi (Yesaya 6:1-2).

Aneneri anauza ena zomwe anadziwa za Mulungu. Mulungu anafuna iwo kudziwa zambiri za iye. Conco anatumidza Mwana wace Yesu. Nthawi inali itakwana, ndipo zonse zinali zitakonzeka. Tikhoza kudziwa bwino Mulungu pamene tidziwa Mwana wace, Yesu, munga Mbuye ndi Mpulumutsi.

KRISTU ABVUMBULUTSA MULUNGU KWA MUNTHU

Yesu anali ndi Mulungu kucokera pa ciyambi ca nthawi (Yohane 1:2). Ahebri 1:3 itanthauza kuti Kristu ndi cikaniziro ca Mulungu. Pamene tidziwa Yesu tidziwa Mulungu (Yohane 14:9). Yesu ali munga Mulungu mu njira iliyonse. Ali ndi mphamvu. Akhoza kukhululukira cimo. Mulungu anapatsa Mwana wace malo a ulemu ndi a mphamvu m'mwamba.

Angelo ndi athenga a Mulungu. Iwo analengedwa kutumikira Mulungu. Koma Yesu si mngelo, Yesu ndi Mwana yekhayo wa Mulungu. Yesu apambana angelo. Mulungu afuna anthu kumudziwa. Afuna iwo kukhulupirira mwa Yesu. Mulungu afuna inu kukhala mwana wace. Ngati ndinu mwana wa Mulungu, kodi afuna inu kuti mucite ciani?

MULUNGU AFUNA ANTHU KUMVETSERERA KWA IYE

Werengani Ahebri 2:1-9. Pamene Mulungu analankhula kwa anthu ace kupyolera mwa angelo ndi aneneri, anawayembekezera kumvera iye. Pamene iwo sanamvere Mulungu, anawalanga. Pamene ana amalephera kumvera atate ao a pano padziko lapansi, amalangidwa. Ndi cimodzi-modzinso ndi ana a Mulungu.

Pamene Yesu anadza pa dziko lapansi, anthu ambiri anamvetsera kwa iye. Ena amene anamvera iye, anawakhululukira macimo ao. Anasintha miyoyo yao. Onse amene anakhulupirira mwa iye anapulumutsidwa.

Mulungu anagwiritsa nchito anthu amene adziwa Mwana wace kuuza ena za Yesu. Kodi Yesu ndi Mpulumutsi wanu? Ngati ndi tero, Mulungu ayembekezera inu kumvera iye.

MULUNGU ASAMALIRA ANTHU ONSE.

Ngati Mulungu sakanakonda munthu, sakanamulenga iye mu cifaniziro cace, (Genesis 1:26). Mulungu anapanga munthu kulamulira pa dziko lonse. Patapita nthawi anatumidza Mwana wace Yesu pa dziko. Nakhala ndi moyo, nabvutika, ndipo anafa pa mtanda, cifukwa ca macimo a anthu onse. Yesu anauka kwa akufa kuti onse okhulupirira apulumutsidwe.

Mulungu asalimalira anthu onse kopanda sankho. Mulungu afuna anthu onse kupulumutsidwa.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Kodi mufuna kumdziwa Mulungu? Coyamba, muyenera kutembenuka ku macimo anu ndi kulandira Yesu monga Mpulumutsi wanu. Mukhoza kudziwa za Yesu kopanda kudziwa Yesu. Kodi Mumvetsa ici? Mukhoza kudziwa za munthu odziwika kwambiri amene anafa kale; koma simukhoza kumdziwa munthuyo, cifukwa anafa.

Mu njira imodzi-modzi, mukhoza kudziwa za Yesu yemwe anakhala pa dziko zaka zambiri zapitazo. Koma kofikira mutamulandira monga Mpulumutsi wanu, simudzamudziwa Yesu. Iye ali wakufa kwa inu. Iye akhala wa moyo kwa inu pamene alowa mu umoyo wanu monga Mbuye.

Mutalandira Yesu monga Mbuye, muyamba kumudziwa iye. Pamene muphunzira mau ace tsiku ndi tsiku ndi kupemphera, mumdziwa bwino. Pamene mumkhulupirira, mumdziwa bwino. Muyenera kufunitsitsa kudziwa Yesu. Iye azibvumbulutsira yekha, kwa iwo amene ayetsa kumulondola.

Tidziwa bwino Mulungu kupyolera mwa Yesu. Yesu ndiye njira, moyo ndi coonadi. Palibe abwera kwa atate koma mwa Yesu. Kodi mwakhulupirira Yesu monga Mpulumutsi wanu?

MUTU 13

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Mulungu ndi iye yekha yemwe tikhoza kukhulupirira mokwanira.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Ndifuna ophunzira anga kuzindikira kuti pena ali kuika cikhulupiro cao mu zinthu za cabe. zinthu zacabe. Ndidzawalimbikitsa kukhulupirira Mulungu mokwana.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Bolodi, kapena pepala lalikulu ndi colembelela.

KUPHUNZIRA KOYAMBA:

Zinthu zomwe tidzaphunzira mu phunziro ili zinacitika pa phwando mu caka ca 609 B.C. Dziko la Israyeli inali itagawanika pakati mu caka ca 922 B.C. Mbali ina inasunga dzina la Israyeli, ndipo mbali ina inatenga dzina la Yuda.

Pa nthawi yomwe Yeremiya anali kulalikirira mukacisi (ndiyo nthawi ya phunziro imeneyi) Mbali ina ya Israyeli inali itatengedwa kuukapolo. Cimodzi-modzi cinali kuyembekezera Yuda mu caka ca 587 B.C. Patapita zaka 21 pamene Yeremiya atacenjeza Yuda.

Yeremiya 7:1-15 ili ndi cenjezo la Mulungu. Anena kwa anthu kuti adzawasunga ngati iwo asunga malonjezo ao. Mulungu anafuna kuti anthu ace ayenera kukhala ndi umoyo omwe uonetsa kuti anasankhidwa.

Yeremiya 7:1-4 inena kuti Mulungu anauza Yeremiya kulankhula kwa anthu. Anauzidwa kupita kukacisi, ndi kuimilira pa cipata comwe wansembe anapita ndi kucenjeza anthu. Mulungu anati, "Tembenukani ku macimo anu ndipo ndidzakulolani kukhala mu dziko lino. Musapitilize kukhulupirira mu zicinjirizo za kacisi kuti zidzakupulumutsani kwa Adani anu."

Ansembe ndi aneneri aboza anali kutsimikiza anthu kuti Mulungu sadzalola ciri conse coipa kubwera pa kacisi. Mulungu ananena kuti kunena kwao kwakuti "Ili ndi kacisi la Mulungu." Sikudzawapulumutsa. Anthu anali kukhulupirira kuti zipembedzo zao sidzikanakhoza kukakamiza Mulungu kuwapulumutsa. Yeremiya ananena kuti zipembedzo zao zonse sidzinali zabwino. Pa kucita izi, anaika moyo wace wonse mu manja ace.

"Mu Yeremiya 7:5-7, Mulungu anauza anthu kuti ngati iwo akanafuna kubwerera kucipangano ndi kulondola ziphunzitsa, iye akanawalola kukhala kumene iwo anali. Iye anali kunena "Ndikali kukukondani."

Anthu a ku Yuda anaganiza kuti anafunika kungopita ku kacisi kukapembedza. Yeremiya anawauza kuti Mulungu anafuna iwo kukhala ndi miyoyo yoyera. Mneneri wina, Mika, anawauza zomwe anafuna kuti acite.

ZOMWE MULUNGU AFUNA KWA ANTHU ACE

Werengani Mika 6:6-8. Anthu aku Yuda anaganiza kuti Mulungu anafuna nsembe yambiri. Iwo anacita ici, koma sicomwe Mulungu anafuna.

Mika anawauza kuti Mulungu anafuna anthu kucita zinthu zitatu:

1. Kucita cilungamo.
2. Kucita zabwino.
3. Kuyenda ndi Mulungu.

Kucita cilungamo citanthauza kuti anafunika kukhala ndi munthu mnzao bwino. Iwo anafunika kukhululukira, kukonda ndi kuthandiza kuyenda ndi Mulungu citanthauza kusamira pa Mulungu, ndi kumukhulupirira.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Mulungu akali kufuna zinthu zimodzi-modzi kwa anthu ace. Afuna ife kumukhulupirira mokwanira. Iye safuna kuti ife tiyembekezere pa ucinjirizo wabodza.

Kodi muli ndi ucinjirizo wabodza mu umoyo wanu? Kodi muli kukhulupirira kuti mpingo udzakupulumutsani? Kapena mukhulupirire kuti ndalama zanu, munda kapena banja lanu ndi abwenzi adzakucinjirizani? Zinthu zonse izi zikhoza kulephera.

Bwanji osakhulupirira Mulungu? Iye apatsa ucinjirizo wa muyaya. Ngakhale mutakhala Mkristu, mukhoza kusakhulupirira Mulungu mokwanira.

Cimo mu umoyo wathu ileza kupembedza Mulungu mu coonadi. Mulungu afuna ife kumukhulupirira. Mulungu safuna ife kukhulupirira mu zinthu zomwe sizili zoon. Afuna kuti tikhulupirire iye yekha. Mulungu alonjeza kutisamalira ngati titumikira iye masiku onse.

MUTU 1

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Munthu akhoza kudziwa bwino Mulungu pa kudziwa Mwana wace, Yesu Kristu.

COLINGA CA KUPHUNZITSA: Ndifuna ophunzira anga kudziwa kuti njira imodzi yokha yomwe iwo akhoza kudziwa Mulungu ndi kupyolera mwa Yesu.

ZOTHANDIZIRA PAKUPHUNZITSA: Palibe.

KUPHUNZIRA KOYAMBA:

Buku la Ahebri linalembedwa ku gulu la Akristu oyamba omwe anali atayamba kutengedwa ndi zikhulupiriro zina. Buku linalembedwa ndi munthu wosadziwika yemwe anaitana Akristu aja ku cikondi comwe anali naco poyamba. Kucita ici anakumbutsa owerenga kuti Kristu ali opambana aneneri ndi angelo.

Mu ndime izi, anena kuti anaika nzeru zao kwa angelo. Pa nthawi ya kulemba bukuli, cikhulupiriro ca angelo cinali kukula. Anthu anaganiza kuti angelo anali kuimirira pakati pa anthu ndi Mulungu. Mlembi anafuna kuti anthu adziwe pamene Kristu anali ndi angelo. Ahebri 1:1-4 ndi mndandanda wabwino wa ndime zomwe ziri ndi uthenga. Mlembi anena kuti Mulungu anagwiritsa nchito njira zambiri kulankhula ndi Mulungu. Mulungu anazionetsera iye yekha kwa anthu kupitira mwa aneneri. Anali kuzionetsera pang'ono pang'ono.

Kupitira mwa Elisha, Mulungu anauza mtundu wa anthu kuti iye yekha anali Mulungu. Yesaya analoledwa kunena za kuyera kwa Mulungu. Amose anagwiritsa liu la mphamvu kunena kuti Mulungu ndi wopanda sankho. Iye adzawalanga ngati anthu samvera iye. Yeremiya analira pamene anaona momwe Mulungu adzaweruzila anthu. Hoseya anagwiritsa nchito ayumba yace kuonetsa cithunzi-thunzi ca Mulungu kuti anali wokhululukira.

Wolembe apitiriza kunena kuti cibvumbulutso comwe anauza kwa aneneri sicalinali cokwanira, koma cibvumbulutso cinakwaniritsidwa mu Mwana wa Mulungu. Ananena kuti Kristu, Mwana wa Mulungu, ndi colowa ndiponso Mlengi. Amaonetsa ulemelero wa Mulungu. Kristu ndi cifaniziro ca Mulungu. Agwiririra dziko lakumwamba pamodzi. Mphamvu yace ndi cimodzi-modzi ndi mphamvu ya Mulungu. Mwana wa Mulungu amayeretsa munthu ku cimo. Iye ali ndi ulamuliro wa kukhala kudzanja lamanja la Mulungu. Dzina lace ndi yaikulu kupambana angelo onse.

Ahebri 1:5-14 ndi mndandanda wa ndime za m'Cipangano Cakale. Colinga cace ndi kuonetsa kuti Kristu ndi wamkulu kupambana angelo. Mlembi anafunsa ngati panali wina yemwe anachedwa Mwana wa Mulungu. Potsiliza anati, angelo ali mizimu yomwe ili kufalitsa uthenga pa dziko.

Ahebri 2:1-9 ndi mau abvuta. Mlembi anacenjeza Akristu kuti asacoke ku uthenga omwe analandira kwa Mulungu.

Cipulumutso cimapitirirabe. Anthu ambiri aganiza kuti atalandira Yesu Kristu, palibe cina cocita. Ena ayembekezera kugawana ulemmero wa Mulungu, koma alephera kugawana uthenga ndi anthu otayika owazungulira. Cipulumutso ciri ndi ciyambi (kalandira Kristu) kupitiriza (kukula ndi kulondola Kristu masiku onse.) Anthu a Cihebri sanali kukula. Ici ndico cinabvuta mtima mlembi. Iye anafuna kuti iwo akule.

Mlembi wa Ahebri anacotsa mau mu Salmo 8 omwe ali mau akunena za munthu yemwe anafunikira kukhalira. Munthu anafunika kukhala olamulira pa dziko. Munthu analephera kukwaniritsa colinga. Werengani Ahebri 2:8. Tiona Yesu, ndipo kupyolera mwa iye tikhoza kubwerera kumalo komwe Yesu anafuna kuti ife tikhale. Mwana wa Mulungu anabvutika ndipo anafa, kuti ife tisalawe imfa (Kusiyana ndi Mulungu).

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Nenani: "Maphunziro otsatira asanu, tidzaphunzira buku la Ahebri. Buku ili linalembedwa kuitana Akristu ku uthenga wa cipulumutso. Ambiri aiwo anali atacoka kuziphunzitso zomwe anaphunzira, Iwo anali atayamba kukhulupirira kwambiri mwa angelo ndi mphamvu yao. Sitidziwa bwino amene analemba buku ili. Koma tidziwa analemba kukumbutsa Akristu kuti Yesu anali wamkulu kupambana aneneri kapena angelo. Mu kalata yace, anafuna kuwakumbutsa za cikhulupiriro cimene iwo anali naco.

KUMASULIRA

Uzani ophunzira kutsegula ma Buku Opatulika ao ku Ahebri 1:1. Wina awerenge ndime 1-4. Funsani "Kodi tikhoza kudziwa bwani Mulungu? Aloleni alankhuzane. Onani kuti ophunzira adziwa kuti adziwa Mulungu kupitira mwa Yesu.

Nenani: "Mu Cipangano Cakale, anthu anadziwa Mulungu kupyolera mwa aneneri. Mulungu anagwiritsa nchito aneneri ambiri pa nthawi yosiyana siyana kuuza anthu za iye. Anakhoza kuwauza pang'ono za iye. Munthu sanakhoze kuzindikira zonse za Mulungu. Conco pang'ono pang'ono Mulungu analankhula kwa munthu, kumuuza kuti anali oyeri, okhululukira, wosakondera, ndi olanga omwe analephera kutsatira, ndi kuti awakonda.

anacenjeza Yuda, kulapa ndi kubwerera kwa Mulungu. Koma mtundu umenewu unaganiza kuti panalibe comwe cikanacitika kwa iwo cifukwa kacisi wa Mulungu unali mu Yerusalemu. Iwo anakhulupirira kuti Mulungu sakanalola cinthu coipa kuononga nyumba yace.

Yosiya anali m'modzi wa mafumu a Yuda. Anali mfumu yabwino, ndipo anayesa kubwezera anthu kwa Mulungu. Anthu sanamvere, posacedwa anaiwala mau a Yosiya.

Yeremiya anadziwa kuti mbali ina ya Israyeli inagwa. Anadziwa ici cifukwa anali atatembenuka kucoka kwa Mulungu. Mulungu analankhula ndi Yeremiya ndi kumuuza kucenjeza mtundu wa Yuda. Werengani Yeremiya 7:1-15.

Yeremiya anauza mtundu kuti usaike cikhulupiriro mwa kacisi. Cinamangidwa ndi manja a munthu, ndipo cikhoza kupasulidwa ndi manja a anthu.

KUITANIDWA KUTI ALAPE

Ndipo Yeremiya anauza anthu aku Yuda ".....lungamitsani njira zanu ndi zocita zanu" (Yeremiya 7:3). Iwo anafunika kulapa ndi kusiya kucita zoipa. Kupita kukacisi sikunali kokwanira. Anafunika kutumikira Mulungu masiku onse.

Anafunika kukhulupirira Mulungu mu njira zabwino. Sanafunika kusautsa alendo ndi amasiye. Anafunika kukhala okhulupirika kwa Mulungu. Mulungu anakwiya cifukwa ambiri anali kulondola milingu yabodza.

LONJEZO LA MULUNGU

Mulungu anapanga lonjezo kwa anthu a ku mtundu wa Yuda. Ananena kuti ngati analapa ndi kukhala okhulupirika kwa iye. Akanawasunga mu dziko lolonjezedwa. Akanawatetdeza kwa adani. Ngati iwo analephera kusunga lonjezo kwa Mulungu, iwo adzatengedwa kuukapolo monga mbali ya Israyeli ina.

Mulungu anaonetsaso cikondi cace kwa anthu. Panalibe kanthu ngakhale anapitiliza kucimwa, iye anawakondabe.

Yeremiya anafuna anthu kumvetsetsa zonse zomwe zinali zofunikira. Anawafunsa mafunso.

1. Kodi iwo anafuna kupitiliza kucimwa?

2. Kodi anafuna kupitiliza kuswa pangano la Mulungu pa kucita cigololo, kupha, kuba, kunama bodza ndi kupembedza milungu ina?

MUTU 13

ZIOPYEZO ZA UCINJILIDZO WABODZA

COLINGA: Phunziro ili idzandiphunzitsa kuti ndiyenera kuika cikhulupiro canga conse mwa Mulungu ndi kukana zicinjilizo zabodza za m'dziko.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Yesaya 30:1-7; 31:1-3 Yeremiya 7:1-15; Mika 6:6-8

NDIME ZA MPHUNZIRO YA LERO: Yesaya 31:1-3 Yeremiya 7:1-15, Mika 6:6-8

MAU APAMTIMA: *"Ndicabwino kuthawira kwa Ambuye kupambana kuika cikhulupiro mwa munthu."* (Salmo 118:8)

Anthu amakhulupirira mu zinthu zambiri zosiyana-siyana. Munthu akhoza kumvera bwino ndipo ocinjirizidwa cifukwa ali ndi nchito yabwino. Kodi akhoza kucita ciani atacotsedwa nchito?

Wina akhoza kuganiza kuti ali ocinjirizidwa cifukwa ali ndi thupi la nthanzi. Koma matenda amabwera mwadzidzidzi. Tsopano cidzicitika nciani?

Anthu akhoza kuika ndalama zao ku banki, ndi kuganiza kuti ali ocinjirizidwa. Koma nthawi zina banki imalephera ndipo ndalama zimapita.

Mkazi akhoza kukhala ndi mwamuna wabwino yemwe amsamalira. Amaganiza kuti ali ocinjirizidwa. Palibe codandaulitsa. Koma mwamuna wace akufa ndi kumusiya kopanda ndalama.

Kodi anthu akhoza kukhulupirira ciani comwe sacidzawalepheretsa? Phunziro ili idzatiuza.

ISRAYELI NDI YUDA

Mtundu wa Israyeli siunali kugwirizana. Mbali ina ya Israyeli inapembedza mafano. Anapembedza zopanga ndi manja. Iwo sanafune kupembedza Mulungu. Anaganiza kuti Mulungu sadzawalanga. Palibe mwa mafumu onse 19 anayetsa kuwabweza kwa Mulungu. Mbali iyi inasunga dzina la Israyeli.

Mbali ina inasankha dzina la Yuda. Iwo analondola mbadwo wa Davide. Anapembedza Mulungu, ena mwa iwo anapembezanso mafano. Ena mwa mafumu aja anayesa kubweretsa anthu kwa Mulungu.

Israyeli, mtundu wa mbali ina, unaganiza kuti unali wocinjirizidwa. Koma unalephera msanga. Iwo anatengedwa kuukapolo ndi a Siriya. Yeremiya

Pang'ono pang'ono munthu anakhoza kutenga cithunzi-thunzi ca Mulungu. Cinasalira kwa Yesu kuonetsera Mulungu kwa anthu mokwana."

Funsani "Kodi Mulungu amazionetsera bwanji iye yekha kupyolera mwa Yesu?" Kaciwiri, apatseni nthawi. Aloleni anene kuti palibe angadziwe Yesu pokhapo atamlandira monga Mpulumutsi.

Funsani "Pamene titalandira Kristu monga Mpulumutsi, kodi timamudziwa mokwana?" Mumalankhulidwe anu nenani kuti ndi cofunikira kulondola Yesu masiku onse, kukhulupirira mau a Mulungu, kuwerenga ndi kupemphera.

Pemphani wophunzira kuwerenga Ahebri 2:1-9. Wina amasulire ndime 1, wina ndime 2, wina 3 wina 4. Funsani kuti mphatso za Mzimu Woyera ndi ciani?

Nenani: "Ndime 5-9 Icokera mu Salmo 8" Wina apeze ndi kuwerenga ndime imeneyi. Nenani: "Mulungu analenga munthu kulamulira dziko lino, koma munthu analephera kucita zomwe Mulungu anayembekezera. Conco Yesu anabwera kudzafa kuti Mulungu akakhoze kubwezera munthu pamalo ace. Ndime yotsiliza icotsa maso athu pa anthu ndi kuwaika pa Yesu, yemwe anatifera.

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Funsani: "Kodi ndi cifukwa ciani ndime izi ziri zofunikira masiku ano? Apatseni nthawi alankhuzane. Mufuna kuti adziwe kuti njira imodzi yokha ndi kupyolera mwa Yesu Kristu.

Nenani: "Kodi tiri ophunzira omwe Yesu afuna kuti tikhalire? Kodi tiri kumulondola monga momwe afunira? Kodi pali mbali ina pomwe tifunika kusintha kuti tidziwe Mulungu bwino kupyolera mwa Yesu?

Tsekani mtsonkhano ndi pemphero. Pemphani Mulungu kuonetsera ophunzira aliyense zomwe afunika kucita mu umoyo wace.

MUTU 2

YESU, WANSEMBE WATHU

COLINGA: Ndidzaphunzira phunziro ili kuti ndimvetsetse momwe Yesu akhalira mkulu wansembe pakati pa ine ndi Mulungu.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Ahebri 2:10-5:10:

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Ahebri 4:14-5:10

MAU APAMTIMA: *"pakuti sitiri naye mkulu wa ansembe wosatha kumva cifundo ndi zofoka zathu; koma wayesedwa m'zonse monga momwe ife, koma wopanda ucimo."* (Ahebri 4:15)

Ku dera ina komwe kunali nkondo, gulu laling'ono la azibambo, azimai ndi ana mwamsanga anathamangira mu chire. Akulu-akulu anali kuyang'ana kumbuyo kuona ngati panali ena amene anali kuwalondola. Ngati mwana wina wagwa anali kunyamulidwa mwamsanga ndi amai ace. Mtsogoleri anadziwa kuti gulu linali litatopa kupitiliza ulendo.

Mwadzidzidzi, kutsogolo kwa mtsogoleri, pansi panatseguka. Panali dzenje lalikulu. Amuna anakhoza kulumpha, koma azimai pamodzi ndi ana sanakhoze kulumpha. Mtsogoleri wao anaitana azibambo ndi kulankhulana nao. Ndipo iwo anathamanga pamodzi ndi kulumpha dzenje lija. Kumbali ina anagwirirana ndi kufika pafupi ndi dzenje.

Mtsogoleri anaitana azibambo awiri kugwira miyendo yace, ndipo iye anagona pakati pa dzenje limenelo. Azibambo anai aja anagwira manja ace. Mtsogoleri uja anali atapacikidwa pakati pa zenje. Amuna anathandiza ana kuyenda pa mwamba pa thupi lace. Azimai naonso analondola, atatha mtsogoleri uja anaguzidwa ku tsidya lina. Amuna aja otsiliza analumpha kumbali ija.

Ndipo gulu linabisala mwacete mu chire. Pamene adani anafika pa dzenje lija, iwo anaganizira kuti azimai ndi ana sanaoloke. Iwo anagawanika ndi kuyamba kufuna-funa mu mitengo pafupi ndi dzenje.

Gulu laling'ono lija mwamsanga linapitiliza kupita ku mbali ina ya dzenje.

YESU NDI ULALO WATHU

Phunziro lathu lero litiiza kuti Yesu ndi wansembe wathu. Wansembe ndi ulalo pakati pa Mulungu ndi anthu. Iye amapangitsa anthu kuti aoloke. Mu Cipangano Cakale, wansembe anali munthu wapadera. Iye anali kuimilira anthu

agogo ace cifukwa ca kulakwa kwa abambo wace, koma ambiri anatero. Ndipo iwo anayembekezera Solomoni kukhala monga atate wace."

Funsani: "Kodi nthano iyi ikhoza kucitikadi? Apatseni nthawi alankhuzane.

Ndipo nenani: "Phunziro lathu lero icokera mu Ezeikieli 18 ndipo itiuza yemwe afunika kutenga cilango ca macimo ace.

KUMASULIRA:

Uzani Ophunzira anu kutsegula Mabuku ao Opatulika ku Ezeikieli 18. Nenani: "Phunziro lathu lero ndi la nthano yomwe mwamva. Mbali ya iyo ndi ya kulungama kwa agogo, mbali ina ya kucimwa kwa mwana ndipo mbali ina ya mwana wolungama. Tiyeni tiwerenge ndime 1-4, "Inu aphunzitsi mukhoza kuwerenga."

Nenani: Mtundu wa ana a Israyeli unali ku ukapolo ku Babulo. Iwo anakhala komweko zaka 50. Kutengedwa ku ukapolo kunali cilango comwe Mulungu anapatsa ku mtundu wonse. Mtundu unali utacimwa, pa kuswa ciyanjano ndi Mulungu. Mulungu anawacenjeza kuti adzawalanga pa zomwe anacita, iwo anali osalungama.

Anaganiza kuti anawalanga mosayenera kuti anapanga mwambi. Tawerenga kale za mwambi umeneu. "Kodi citanthauza ciani kunena kuti mano a mwana anayayamira cifukwa atate ace anadya mphesa zosacha?" Lankhuzanani pa izi. Thandizani ophunzira anu kudziwa kuti kudya mphesa zosacha cipangitsa mano kumveka mwina-mwina. Ici cinanena kuti macimo ya atate anagwera mwana.

Nenani: "Mulungu anatumiza Ezeikieli kuuza anthu kuti analakwa. Cilango sicipatsidwa kucoka kwa tate kupita kwa mwana. Tiyeni tiwerenge zitsanzo zitatu zomwe Ezeikieli anapatsa. Wina awerenge ndime 5-9 "Gwiritsani nchito mau ali pa kuphunzira koyamba. Kumasulira ndime izi." Munthu wolungama anali ngati agogo ace a Solomoni mu nthano yomwe tamva.

Pemphani wina kuwerenga ndime 10-13. Nenani "Ndime izi ndi za mwana wocimwa omwe tikhoza kulinganiza ndi abambo wace a Solomoni." Gwiritsani mau ali pa kuphunzira koyamba. Kukuthandizani kumvetsetsa ndime izi Nenani: "Ndime ya 20 ndi kumasula kotsiliza kwa ziphunzitsa za Ezeikieli. Munthu aliyense adzalangidwa pa macimo ace." Werenganinso ndime.

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU:

Funsani: "Kodi mumaganizapo kuti mumalangidwa pa macimo a munthu wina? Mkazi yemwe ali ndi mwamuna yemwe akumwa mowa amabvutika. Nthawi zina timabvutika pa macimo a munthu wina, koma sicilango ca Mulungu pa ucimo. Sitiyenera kunamizila Mulungu."

Tengani nthawi ya kulankhuzana ndi kutsiliza ndi pemphero.

Munthu wangwiro asunga lamulo. Zicitilo zomwe zichulidwa mu ndime izi ndi zomwe zinazindikiridwa monga zoyera mu lamulo. Ngati munthu anafuna kuonedwa kuti anali oyera, anafunika kusunga lamulo lonse.

Ezekieli 18:10-13 ionetsa mtundu watsopano. mwana wocimwa ali ndi tate wangwiro, koma ubwino wa atate wace siunakhuze mwana. Iye sanapatsidwe mphoto cifukwa ubwino wa atate wace.

Mwana woipa uja anakana zonse zomwe atate wace anasunga. Anacita zoipa kwambiri, ngakhale kupha.

Mwana wocimwa adzafa cifukwa ca macimo ace. Anacimwira dala. Tsopano adzalipila mtengo wa macimo. Atate ace sakhoza kumupulumutsa ngakhale ndi macitidwe ao.

Ezekieli 18:14-20 itibweretsa ku mtundu wa citatu. Mwana uyu ndi wangwiro. Pena anaphunzitsidwa ndi agogo ace. Pena anaona zoipa za atate ace, ndipo anaganzira kuti sanafune kutengako mbali. Anasankha ubwino mu umoyo wace.

Mwana woyera ali ndi mphoto cimodzi modzi monga ya agogo ace. Iye sakhuzidwa ndi ucimo wa atate ace. Iye adzakhala ndi moyo cifukwa ali kukhala ndi umoyo wokondweretsa Mulungu.

Mu cikhulupiriro comwe ana a Israyeli anali naco kuukapolo, mwana uyu anafunika kulangidwa cifukwa ca macimo a atate ace. Ezekieli anena kuti ai. Mwana uyu sanacite ciri conse coipa kuti aphedwe. Munthu aliyense adzawerengedwa macimo ace. Azisankhira moyo kapena imfa.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO:

KUDZIWITSA:

NENANI NTHANO IYI

“Solomoni anali khale mnyumba momwe munali mdima, kumvetsera ku mau omwe anali kulankhulidwa kanja. Anadziwa kuti atsilikali anali atabwera kufuna-funa atate ace. Pamene anamva kugogoda pa khomo, anaopa kwambiri. Anakhala cete, pena adzangopita kuganiza kuti mulibe munthu. Ndipo iye adzapita kwa agogo ace kukabisala. Anakumbukira pamene atsilikali anali atabwera tsiku lina. Anampanda kwambiri cifukwa sananene kumene kunali abambo ace.

“Patapita nthawi phokoso inatha. Anayembekezera pan’gono, ndipo anafuna kuyamba kuthamanga kwa agogo ace. “Ncifukwa ninji anaganiza atate ace anali mbala? Anazifunsa yekha. Aliyense anadziwa kuti agogo ace anali munthu wabwino. Solomoni anali kuyesa kukhala monga iwo. Palibe anafunika kunena

kwa Mulungu. Koma wansembe m’meneyu analinso munthu. Anali kucimwa monga anthu onse. Mbali ya nchito yace inali ya kupereka nsembe kwa Mulungu ya macimo ace ndiponso ya anthu ace. Wansembe anayesa kuphunzitsa anthu za Mulungu, koma analephera. Anayesa kuthandiza anthu, koma anafunikanso thandizo lalikulu.

Yesu ndi wansembe wathu. Iye amathandiza anthu. Amatiphunzitsa za Mulungu. Amatithandiza kumvetsetsa za Mulungu, cifukwa ndi Mulungu. Iye analibe cimo, conco akhoza kukhululukira macimo athu.

Akristu ali ndi danga ndi madalitso ambiri cifukwa tiri ana a Mulungu. Pamene tilandira Yesu monga mpulumutsi, iye akhala wansembe wathu. Pamene ticimwa ndi kupempha cikhululukiro Yesu amakhalapo mwa Mulungu kupempha Mulungu kuti khululukira.

GWIRIRIRANI KU CIKHULUPIRIRO CANU

Mu Ahebri 4:16-5:10 Akristu auzidwa kugwirira kucikhulupiriro cao. Ngati tigwirira kucikhulupiriro cathu, timacigwiritsa masiku onse cimakula. Tifuna kucotsa cimo mu umoyo wathu.

Yesu adziwa kuti tiri ofoka. Adziwa kuti tidzacimwa. Amatimvetsetsa ife. Afuna kutithandiza. Pamene timuza macimo athu, atikhululukira ndi kutipatsa cifundo ndi cisomo cace. Izi ndi mphoto zathu zabwino zomwe zicokera kwa wansembe wathu, atipatsa cikhululukiro, cifundo ndi cisomo.

Yesu ndi ulalo wathu, ulalo wathu ndi wa kwa Mulungu. Adziwa mabvuto athu ndi kufoka kwathu. Iye ali pano kutithandiza.

MKULU WANSEMBE WA MU CIPANGANO CA KALE

Mu nthawi ya m’Cipangano Cakale, kunali ansembe ambiri, koma kunali ansembe akulu ang’ono. Kodi zofunikira zace kuti ukhale wansembe zinali zotani?

1. Iye anafunika kuitanidwa ndi Mulungu. Anafunika kukhala Myuda. Anaitanidwa kuimilira anthu kwa Mulungu. Anafunika kuyesa kumvetsetsa anthu ndi kuwathandiza.

2. Iye anafunika kupereka nsembe ya macimo ace ndi ya anthu ace. Wansembe anafunika kupereka nsembe ya macimo ace. Ndipo anafunika kupereka nsembe ya macimo a anthu ace.

Kukhala wansembe inali nchito yaikulu. Palibe amene afuna nchito yobvuta! Anasankhidwa kucita nchito imeneyi. Mulungu anasankha Yesu ndi kumuuzwa kuti ali "Wansembe wa muyaya! Nthawi zonse adzakhala wansembe wathu.

Melekizedeki anali wansembe wa mkulu wa Mulungu. Abrahamu anapereka cakhumi kwa iye (Genesis 14:18-20). Mulungu anaitana Melekizedeki kukhala wansembe. Anali odziwika kwambiri. Koma Yesu ali opambana Melekezedeke.

Pamane Yesu anafika pafupi ndi mtanda, anapemphera mokweza "Mofuula ndi misozi" kwa Mulungu. Anadziwa kuti anali Mulungu yekha akanakhoza kumupulumutsa ku imfa. Koma cifukwa anali womvera kwa Atate wace, analandira imfa yace pa mtanda.

Yesu atimvetsetsa ife. Iye amvetsetsa mabvuto athu. Iye anapitamo mu mabvuto athu, ndipo iye sanacimwe.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Yesu afuna anthu ace okhulupirira mwa iye komvera iye. Afuna kuti timvere iye. Atipulumutsa kumacimo athu. Adzatikhulukira macimo athu. Conco, tiyenera kukhala ozicepetsa ndi kumvera Yesu.

Kumbukirani munthu yemwe anakhala ulalo kuti apulumutse anthu ace? Werengani mau omwe ali pa kudziwitsa a phunzire ili kaciwiri. Yesu ali ngati munthu uja. Anazipereka iye yekha kukhala ulalo wa munthu kufika kwa Mulungu.

Kodi mukali ndi cimo mu umoyo wanu? Kodi mudzapempha Yesu kukukhulukirani? Kodi mudzamvera? Afuna kukuthandizani kuti mukhale ndi umoyo womvera, umoyo wokondwa. Ali kuyembekezera inu kunena, "Cifuniro canu cicitidwe."

MUTU 12

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Munthu aliyense azisankhila yekha.

COLINGA CA KUPHUNZITSA: Ndifuna ophunzira anga kuzindikira macimo ao. Ndifunanso kuwadziwitsa kuti macimo ao akhoza kukhululukidwa ngati apempha Mulungu.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Palibe

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Ezekieli 18 inapatsa anthu a Ciyuda kuona mwa tsopano pa cimo lao. Mu Buku Lopatulika lonse tipeza nthawi ina pamene Mulungu anaonetsa anthu zocita zao. Tsopano anthu anali atayamba kugazira kuti Mulungu anali kuwalanga pa macimo a makolo ao. Iwo anali atayamba kuganiza kuti Mulungu sanali wabwino.

Mutu uwu uanalembedwa kucotsa mwambo omwe anthu anali nao, ndi kuonetsa maimililidwe a Mulungu poyera. Munthu aliyense anazunzidwa pa macimo ace. Zipatso za kukhala umoyo wabwino ndi kulanga anthu cifukwa ca macimo ao sikukhoza kupatsidwa ku mtundu ndi mtundu.

Ezekieli 18:1-4 uli ndi mwambo wakuti Mulungu ndi wolakwa. Mano a mwana sangayayamire cifukwa cakuti atate ace anadya mphesa zosaca. Mulungu analamulira kuti mwambo uwu ucotsedwe mu maganizo ao. Mulungu awauza kuti onse adzawerengera macimo ace. Mzimu uli wonse ndi wa Mulungu. Ici cionetsa kuti munthu aliyense ali pa yekha pamaso pa Mulungu. Mulungu pamene wina acimwa, munthu una acimwa yekha.

Mulungu anena kuti mzimu omwe ucimwa udzafa. Sadzafa cifukwa ca macimo a munthu wina. Adzafa cifukwa iye anacimwa. Ici cikumbutsa ziphunzitso za cipangano catsopano kucokera ku Aroma 6:23 kuti mphoto ya ucimo ndi imfa.

Ezekieli agwiritsa nchito zithunzi-thunzi zitatatu kumasulira nzeru yatsopano pa kuona pa ucimo. Coyamba ananena za munthu woyera mu ndime 5-9. Ndipo ananena za mwana wocimwa wa munthu wangwiro mu ndime 10-13. Potsiliza anabwera kwa mzukulu wa munthu wolungama mu ndime ya 14-18.

Ezekieli 18:5-9 atiuza zomwe munthu wangwiro acita. Ili ndilo lingo lomwe Ezekieli anasunga, munthu wangwiro adziwika pa zomwe anacita.

UCIMO ULANGIDWA

Mu Ezeieli 18:10-13, Mneneri anaika mu mundandanda macimo omwe adzalangidwa ndi Mulungu. Koma anati, munthu yemwe anacimwa ndiponso yemwe akhala ndi umoyo woipa adzalagindwa. Tate sakhoza kulangidwa cifukwa ca macimo a ana ace. Munthu aliyense adzalipira macimo ace.

Mulungu amapatsa munthu danga kuti alape. Mu Ezeieli 18:30-32, Mulungu anati adzaweruza monga mwa kakhalidwe ka umoyo wa munthu. Ndipo Mulungu anati, "... lapani ndi kutembenuka ku macimo anu...". Muyambe ciyambi ndi umoyo watsopano. Cifukwa sindikondwera mu imfa ya munthu aliyense atero Mulungu, conco tembenukani ndi kukhala ndi moyo.

Kodi uthenga wa Mulungu ndi wotani? Lapani ndi kutembenuka ku macimo. Lapani ndi kukhala ndi moyo. Lapani ndi kukhala ndi mtima watsopano. Lapani kuti mukhululukidwe.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Mulungu akali kufuna munthu kuti alape. Afuna kutikhululukira. Iye anakonzekera njira ya Cipulumutso kwa onse okhulupirira mwa Yesu. Tsopano tikhoza kukhala umoyo wamuyaya ndi Mulungu.

Kodi mufunika ksintha muumoyo wanu? Kodi mukumbukira phunziro la mutu 10 mu buku ili? Mulungu ali nafe nthawi zonse. Atidziwa bwino. Sitikhoza kubisa kanthu kali konse kwa iye. Afuna kuti ife tikhale oyera monga momae iyeb ali. Kodi mulinganiza bwanji colinga ca Mulungu pa umoyo wanu?

MUTU 2

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Yesu ndi mkulu wansembe wathu. Iye aimilira pakati pa Mulungu ndi anthu.

COLINGA CA KUPHUNZITSA: Ophunzira anga adzaphunzira kuti Yesu ndi Mkulu wansembe wathu, yemwe aimilira Mulungu ndi anthu.

COLINGA CA KUPHUNZITSA: Lembani cithunzi-thunzi ca ulalo pa pepala, kapena pa bolodi, kapena mukhoza kubweretsa cithunzi-thunzi ca ulalo.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Ahebri 4:14-16, atidziwitsa kuti Yesu ndi Mkulu wansembe wathu. Liu lakuti wansembe ndi liu imodzi-modzi lonena kuti ulalo. Umu ndimo wansembe ali. Iye apanga njira pakati pa Mulungu ndi munthu.

Mkulu wansembe ndi yemwe anali kutenga nsembe ya macimo kucokera kwa anthu kupita kwa Mulungu. Anali yemwe anacoka pamaso pa Mulungu kubweretsa cikhululukiro ca macimo.

Yesu ndi mkulu wansembe wathu yemwe anacokera kumwamba. Mkulu wansembe wa pa dziko lapansi anali kulowa mu kacisi mu cipinda coyera, kuimilira anthu cifukwa ca macimo ace ndi ao. Yesu anapita mu imfa kufikira anafika kumpando wa Mulungu. Anakwezekedwa cifukwa iye anafika kumaso a Mulungu.

Tiuzidwa kugwiririra ku cikhulupiriro cathu. Liu iyi ithanthauza kugwira ndi mphamvu. Tiuzidwa kugwira kwambiri ku "cikhulupiriro" cathu, kuti pasakhale comwe cingaticotse.

Mkulu wansembe omwe tiri naye anakwezekedwa, koma sali kutali ndi ife. Zoonadi anabvutika m'malo mwathu. Amamvetsetsa kufoka kwathu, ngakhale iye siofoka. Cifukwa ca ici tikhoza kubwera mwamphamvu pamaso pa Mulungu kulandira cifundo ndi cisomo cace.

Ahebri 5:1-10 ndi ndime zabwino. Alankhula za mkulu wansembe, Melekizedeki. Mlembi anena kuti Yesu anali mkulu wansembe atacoka Melekezedeeki. Kodi munthu m'meneyu anali yani?

Melekizedeki anachulidwa kawiri mu Cipangano Cakale, mu Salmo 110:4 ndi mu Genesis 14:17-20. Mu Genesis anena kuti anali wansembe wamkulu wa Mulungu. Abrahamu anapereka cakhumi cace kwa Melekizedeki.

Palibe zomwe tidziwa za makolo ace. Ici cidabwitsa cifukwa munthu anakhoza kukhala wansembe atacokera ku mtundu wa a Levi. Melekizedeki angooneka ndi kusowanso. Abambo wace ndi amace sachulidwa. Tanthauzo lomwe tiyenera kudziwa ndi lakuti, Melekizedeki anakwanilitsa kukhala wansembe, osati cifukwa ca banja lace, koma cifukwa ca kukwaniritsa zofunikira. Iye analibe ciyambi ndi cimalizilo. Anali wansembe wa muyaya. Yesu ndi wansembe wathu cifukwa ca kukwanilitsa kwace. Ndi mkulu wansembe wa muyaya.

Yesu sanasankhe kukhala wasembe. Anaikidwa ndi Mulungu. Monga momwe a Levi analiri. Pamene Yesu anali padziko lapansi, anamva kufoka monga momwe timamva. Analira mokweza ndi misozi. Anaphunzira kumvera, ndipo kupyolera mu kumvera anakhala wolungama. Monga wansembe wolungama, Yesu anakhala ulalo wathu kwa Mulungu (Ciyambi ca Cipulumutso cosatha)

KUPHUNZITSA PHUNZIRO ILI

KUDZIWITSA

Onetsani ophunzira anu ulalo omwe mwalembe kapena cithunzi-thunzi. Nenani: “Ulalo umatithandiza kupita kumalo komwe sitikhoza kupita. Ulalo wina umapita pa mitsinje yaikulu-ikulu. Sitikhoza kupita ku tsidya lina kopanda kugwiritsa nchito ulalo. Phunziro lathu lero ndi la ulalo wapadera, ulalo wocokera kwa munthu kupita kwa Mulungu.”

KUMASULIRA

Ophunzira atsegule Mabuku Opatulika ao ku Ahebri 4:14 ndipo alondole pamene muwerenga 4:14 kufikira 5:10. Nenani: “Tiyeni tione ndime ya 14 poyamba. Kodi wansembe wathu ndani? “Lolani ophunzira ayankhe. Funsani: “Kodi citanthauza ciani, Yesu anapyola m’mwamba?” Aloleni alankhuzane. Tsilizani pa kuwauza kuti Yesu anafika pamaso pa Mulungu atapyola mu imfa. Masulani kuti mukacisi, mkulu wa nsembe anali kufunika kupita mu nsaru asanafike mucipinda coyera, komwe anapereka nsembe ya macimo ace ndi ya anthu. Funsani: “Kodi cikhulupiriro comwe tiyenera kugwirira ndi cotani?” Lolani kalasi ilankhuzane kufikira atamvetsetsa kuti anayenera kugwira cikhulupiriro cao mwa mphamvu kuti wina asawalande.

Nenani: “Yesu amatimvera cifundo cifukwa ca kufoka kwathu, popeza nayenso ndi munthu. Akumbukira momwe kuwawa kunamvekeru. Amvetsetsa kuti mazunzo ndi ciani. Iye pena anamvetsetsa kuyetsedwa kupambana momwe timvetsetsa ife. Iye anayetsedwa kopambana. Nthawi zambiri pamene yesero ikula kwambiri, munthu amagonjera, Yesu sanagonjere. Ili monga kuwawa, timamva kuwawa kwambiri tisanakomoke. Tikhoza kumva yesero kwambiri

KUYANKHA KWA MULUNGU - CIPHUNZITSO CATSOPANO

Mulungu sanali wokondwa ndi ana a Israyeli, cifukwa anali kugwiritsa nchito mwambi wa bodza. Mulungu anati, “....simudzaonanso cifukwa ca kunena mwambiwu m’Israyeli,” (Ezekieli 18:3).

Ciphunzitso catsopano comwe cinapatsidwa ndi Mulungu kwa ana a Israyeli mu Ezekiel 18:4 Cinali ndi mbali ziwiri.

1. “Miyoyo yonse ndi yanga.” Munthu aliyense ndi wa Mulungu. Munthu aliyense adzayankha kwa Mulungu momwe anagwiritsira umoyo wace.

2. Munthu aliyense, Mzimu uli onse, uyenera kulipira mphoto ya macimo ace. Palibe yemwe adzanamizira makolo ace, abwenzi kapena wina aliyense macimo omwe anacita.

Malipilo a cimo mu Cipangano Cakale anali imfa. (Ezekieli 18:4) malipilo a cimo mu Cipangano Catsopano ndi imfa. Ngakhale masiku ano, ndi imfa, cidzakhala cimodzi-modzi muyaya. Iyi ndi lamulo cabe yomwe Mulungu atipatsa kwa anthu onse nthawi zonse. Koma Mulungu sasiya kulanga cifukwa ca cimo. Iye apitiliza pa kupereka ciyembekezo kwa onse akumvera iye.

MPHATSO YA UMOYO WABWINO

Werengani Ezekieli 18:5-9. Mulungu anauza Ezekieli kuti munthu aliyense adzaweruzidwa pa kacitidwe kace. Sadzalangidwa kaamba ka macimo a makolo ace.

Ezekieli anali kudziwa anthu ace. Mulungu anaika mndandanda wa kacitidwe ka munthu wolungama ndi zinthu zomwe sayenera kucita.

1. Iye sanafunike kulambira mafano.
2. Anafunika kuzisunga kukhala oyera ndi kukhala okhulupirika kwa Mulungu.
3. Iye anafunika kuona anthu cimodzi-modzi
4. Anafunika kuonetsa cifundo.
5. Kudyesa anjala.
6. Kupatsa zobvala kwa anthu osowa.
7. Osacita ndeu
8. Anafunika kumvera Mulungu.
9. Kulondola ziphunzitso za Mulungu mu umoyo wace wonse.
10. Osabela anthu anchito. Munthu yemwe anacita zonse izi, anali wolungama.

MUTU 12

NCHITO YA MUNTHU ALIYENSE

COLINGA: Ndidzaphunzira mu phunziro ili amene ali ndi udindo wa macimo anga.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Ezeikieli 18

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Ezeikieli 18:1-20

MAU APAMTIMA: *“Taonani, miyoyo yonse ndi yanga, munga moyo wa atate momwemonso moyo wa mwana, ndiyo yanga; moyo wocimwawo ndiwo udzafa.”* (Ezeikieli 18:4)

Kodi ndi kangati pamene mumanamizira wina pa kulakwa kwanu? Cioneka munga ndiye cimene anthu amacita masiku ano, kunamizira ena pa kulakwa kwao.

Adamu anati, “Hava anapangitsa ine kutero.” Kucokera nthawi imeneyo, munthu akhala ali kunamizira wina macimo ace.

Lero tidzaphunzira kuti munthu aliyense adzaweruzidwa pa macimo ace. Lero tidzaphunzira kuti munthu aliyense adzaweruzidwa pa macimo ace. Sitikhoza kunamizira wina macimo athu. Tiyenera kuyankha kwa Mulungu pa kacitidwe kathu koipa ndi macimo athu.

Ana a Israyeli anaganiza kuti Mulungu sadzawalanga cifukwa ca pangano lomwe anapangana naye. Anayembekezera Mulungu kulanga adani awo osati iwo. Mulungu amalanga aliyense amene acimwa. Mulungu adzakhululukira cimo, koma tiyenera kupempha cikhululukiro cace.

MWAMBI WABODZA

Mu Ezeikieli 18:2-3, tiwerenga za Mwambi wa bodza. “Atate adadya mphesa zosacha, ndipo mano a ana ayayamira.”

Ana a Israyeli anali kunena kuti anali kubvutikira macimo omwe sanacite. Comwe anali kunena ndi ici “Macimo omwe muli kunena ndi a cibadidwe, sitikhoza kuyasiya tiyenera kucimwa atate athu anacimwa ndipo ucimo unabwera kwa ife tonse. Sitikhoza kuzisintha ife tonkha.”

Ana a Israyeli sanamvetsetse kuti ciweruzo ca Mulungu m’buyomu cinagwa pa mtundu wa Israyeli cifukwa analephera kumvera Mulungu. Iwo anali kunamizira ena macimo ao.

pamene tisanagonjere. Yesu “Sanakomoke” Koma anabvutika kufikila kumapeto ndipo analibe ucimo. Tiona mu ndime 15 ndi mutu 5:2 Mulungu atilonjeza kuti Akristu siayeseledwa popanda njira yothawirapo.

Werengani ndime ya 16 kaciwiri ndipo funsani kalasi kuti limasulire.

Nenani: “Mu Ahebrei 5:1 ndi ndime ya 4-5, tiwerenga kuti Yesu sanasankhe nchito ya wansembe, Mulungu anamuika pamalo amenewa” Ngwiritsani nchito kuphunzira koyamba kumasulira kwa ophunzira anu tanthauzo la “Kulondola pa mbuyo pa Melekizedeki.” Ophunzira awerenge Salmo 110:4 ndi Genesis 14:17-20.

Nenani: “Pamene Yesu anali padziko lapansi, anapemphera kwa Mulungu kuti acite zinthu zina. Pamene inafika nthawi kuti afe, anapempha Mulungu kuti amupulumutse ku imfa. Kulira kwace kunali kwokweza ndi misozi. Pamene Mulungu anakana “Kulola cikho kumupitilira” Yesu analola kumwa. Cikho cimene Yesu anapempha kuti cimupitilire inali imfa pa mtanda. Cifukwa ca kuzipereka kwace ndi kumvera, anapangidwa kukhala wa ngwiro. Iye akhala mkulu wa nsembe wathu ndipo ciyambi ca cipulumutso ca muyaya.”

Funsani ngati pali mafunso. Yankhani omwe afunsidwa, kugwiritsa Buku Lopatulika ndi kuphunzira koyamba.

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Nenani: “Kodi phunziro imeneyi itanthauza ciani kwa ife?” Lolani kalasi lanu kulankhuzana. Athandizeni pa kuwauza kuti Yesu ndi mkulu wansembe, ndipo ndi khomo ya kwa Mulungu. Akumbutseni kuti pamene Yesu anafa pamtanda, cinsalu ca mkacisi cinang’ambika pakati. Ici cinali cizindikiro kuti khomo la kwa Mulungu linali lotseguka kwa aliyense.

Funsani: “Kodi alipo wina yemwe sanalandire Yesu munga Mpulumutsi wace? Ngati ndi tero, ndipempha kuti muganizire kuti Yesu ndi wansembe wanu. Ngati mukhoza, salani kumbuyo pamene anzanu atuluka kuti tilankhuzane.

Pitilizani pa kunena, “Yesu anasankhidwa ndi Mulungu munga wansembe. M’njira imodzi-modzi, Mulungu amasankha anthu kulalikirira uthenga wa Yesu. Ngati munthu asankha kulalikirira kopanda maitanidwe a Mulungu, adzalephera. Adzakomana ndi mabvuto ambiri. Mulungu asankha, osati munthu. Pamene Mulungu aitana, Akristu ayenera kuzindikira kuitana kwa Mulungu. Sitikhoza kudziwa zomwe Mulungu ali kunena pokhapo titatenga nthawi ndi iye. Kulankhula ndi iye ndipo kumvetsera.” Lankhulani ndi ophunzira anu, kuwatsimikiza kuti Mulungu agwiritse nchito mau ace kuti alankhule kwa ife.

Tsekani mtsonkhano ndi pemphero.

MUTU 3

YESU, PANGANO LATSOPANO

COLINGA: Phunziro ili idzandithandiza kumvetsetsa momwe Yesu anakhalira pangano latsopano, njira ya kwa Mulungu.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Ahebri 6:1-10:39

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO; Ahebri 8:7-13, 10:10-25

MAU APAMTIMA: *"Tigwiritse cibvomerezo cosagwendera ca ciyembekezo cathu, pakuti wolonjezayo ali wokhulupirika," (Ahebri 1:10-27)*

Nthawi zambiri sitimamva liu lakuti, pangano koma pakati pa Akristu. Litanthauza pangano pakati pa anthu awiri kapena opambanapo.

Phunziro ili ndi la pangano lomwe Mulungu anali nayo ndi anthu mu Cipangano Cakale ndi momwe linasinthidwira mu Cipangano Catsopano. Tifunika kukumbukira pamene tiphunzira kuti inali njira yokha yomwe Mulungu akanalakhula kwa munthu.

Mulungu anadziwa kuti munthu anali kufunika mau a citonthozo. Anadziwa kuti anthu afunika kudziwa kuti akonedwa. Conco Mulungu anapanga pangano ndi Abrahamu, ana ace ndi azukulu ace. Mtsogolo mwace Mulungu anawapatsa malamulo kupyolera mwa Mose. Anadziwa kuti anthu ace anafunika malamulo kuti akhale bwino. Anthu analonjeza kumvera malamulo ace, koma sanatero. Anaswa lonjezo kwa Mulungu. Tiye tione pangano la Mulungu ndi Abrahamu.

PANGANO LA CIPANGANO CAKALE

Werengani Genesis 12:1-3 Iyi ndi imodzi la mapangano a Mulungu mu Cipangano Cakale pakati pa anthu ndi Mulungu. Pamene Adamu anacimwa mu munda wa Edeni. Mulungu anafuna-funa njira ina yokhaliramo mu ciyanjano ndi munthu. Mau ace mu Genesis aonetsa kuti anasankha mtundu, ana a Abrahamu. Iwo anafunika kutumikira monga ansembe, kubweretsa anthu kwa Mulungu ndi kwa Mulungu.

Mtsogolo mwace ana a Abrahamu anachedwa ana a Israyeli. Mulungu analonjeza zinthu zabwino zambiri kwa Abrahamu "...kuti mukhale dalitso" (Genesis 12:2) Iwo analandira zinthu zabwino mwamsanga, koma ana a Abrahamu anaiwala kuti anafunika kukhala mdalitso naonso. Iwo anali atabvomera kumvera Mulungu. Patapita nthawi, ana Israyeli anaiwala lonjezo lao. Anaiwala malamulo a Mulungu. Iwo anacimwila Mulungu.

kufunika ife kukhala oweruza bwino, osayang'ana pa ndalama kapena kusauka. Cacisanu, kuyera kutilesa ife kunena bodza za wina. Cacisanu ndi cimodzi, kuyera kutiuzwa ife kukonda mnansi wathu.

ZOKHUZA KUUMOYO WATHU

Funsani: "Kodi mukumbukira phunziro lathu la mutu 10? Mufunsidwa kuganizira za moyo wanu ngati mufunika kusintha mbali ya moyo wanu. Ngati mukhoza, ndifuna kuti mugawirane zitsankho zanu. Ndidzakhala woyamba, (Mphunzitsi, nenani zinthu zomwe mwasankha kusintha mu umoyo wanu. Ngati simugawana nao, naonso sadzacita.

Apatseni nthawi yokwanira kuti acite ici. Alimbikitseni mu zitsankho zao zatsopano. Lonjezani kuti mudzawapempherera.

Tsirizani mtsonkhano ndi pemphero ya kuzipereka.

mamembala a m'pingo anapempha iye kucita nchito zambiri, anali kuyang'ana kwa Mariya monga mtsogoleri wao. Posacedwa ici cinayamba kubvuta Estere kwambiri. Anaganiza za Mariya kwambiri ndipo anaganiza cocita.

“Estere anaganiza, “Kodi ngati Mariya sali wabwino monga momwe ena aganzira? Sindikondwera pamene ndiona ambiri ali kupita kwa Mariya kuti awathandize. Munabwera ganizo mwa Estere lakuti Mariya sanali bwino. Koma anafunika umboni weni-weni. Anaganiza kumnamizira kuti sanali wokhulupirika kwa mwamuna wace, kuti anthu asiye kutenga malangizo kwa iye. Amuna ace a Mariya anali kugwira nchito kutali ndipo anali kutenga masabata osabwera kunyumba. Mariya anali kukhala kutali ndi kumpingo conco sicinali cobvuta kunena za bodza za iye.

“Conco Estere anayamba kuthira bodza. Anayamba ndi funso limodzi, “Kodi mwamuna uja ndani omwe tinaona ali kulowa mnyumba mwa Mariya pa tsiku la Ciwiri usiku? Posacedwa bodza la Estere linayamba kubala zipatso.

“Mariya anapitiriza ndi nchito yace ya bwino osadziwa zomwe zinali kucitika.

“Tsiku lina anadabwa pamene anamva abusa ali kunena kuti atule mpando wa kuphunzitsa anyamata ndi atsikana, ndi kulola Estere kupitiriza. Pamene anapita kumtsika, anaona abwenzi a kumpingo ali kulankhuzana, anafika pafupi kuti aceze nao koma onse anamwazikana poona iye. Kodi nciani ciri kucitika? Mariya anadabwa ndipo anali osokonezeka.”

Funsani: “Kodi cinthu coteri cikhoza kucitika mu mpingo mwathu?” Apatseni nthawi pang'ono kuti alankhuzane.

Nenani: “Ngati tifuna kuti umoyo wathu ukhale woyera, sitikhala monga Estere. Phunziro lathu lalero ikhuza umoyo wathu.”

KUMASULIRA

Ophunzira atsegule Mabuku Opatulika ao ku Levitiko 19. Pemphani wina kutsegula ndime 2: Gwiritsani nchito mau ali pa kuphunzira koyamba kumasulira ndime iyi.

Ndipo werengani ndime 9-18 ndi kutanthauzira Ophunzira aonjezere kucokera kumabuku ao kapena ku Buku Lopatulika.

Onetsani malamulo khumi omwe mwalembe. Funsani kalasi kulinganiza mindandanda iwiri. Iwo adzaona malamulo ambiri pa ndime zimenezi.

Nenani: “Mulungu ayembekezera ife kulondola malamulo ace a kuyera. Coyamba, kuyera kufuna kukhala ndi cizolowezi ca kusamalira osauka. Caciwiri, kuyera kuletsa ife kuba, madilu, kunena bodza ndi kulumbira. Cacitatu, kuyera kufuna ife kuti titsatire malamulo onse. Cacinai, kuyera

PANGANO LATSOPANO LOSATHA

Mulungu anadziwa kuti pangano lakale linalephra. Anauza Yereimiya kucenjeza anthu kuti kuzafunika pangano latsopano. Pangano latsopano linali la cikondi ndi kumvera Mulungu.

Werengani Ahebri 8:7-13. Pangano latsopano inapangidwa ndi mwazi wa Yesu. Imfa ya Yesu pamtanda inapanga pangano latsopano. “*Pakuti ici ndi mwazi wanga wa pangano, wothiridwa cifukwa ca anthu ambiri kucotsa macimo.*” (Mateyu 26:28)

Pangano latsopano ikanalembedwa mu mitima ya okhulupirika, iwo sakanaiwala. Pangano latsopano likanawalatsa ku ucimo. Ikanawathandiza kukonda, kutumikira ndi kupembedza Mulungu.

CIFUNDO CA MULUNGU

Mu Ahebri 8:12, tiwerenga za cikondi ca Mulungu. Mulungu analonjeza kukhulukira anthu macimo. “Cifundo” citanthauza Mulungu kuti adzatikhulukira ngakhale sitifunika kuteri. Cifukwa ca cikhulupiriro cathu mwa Yesu, adzacotsa cimo yonse.

Tiri ndi pangano latsopano ndi Mulungu. Tiri ndi moyo watsopano wa cikhulupiriro ndi ciyembekezo. Umoyo watsopano upanga ife kufuna kuthandiza ena.

Umoyo watsopano wopanda mantha. Yesu analonjeza kukhala nafe pamene tikhulupirira mwa iye. Iye ali wokhulupirika. Yesu anapanga pangano latsopano, conco tiri ndi moyo wosatha.

Werengani Ahebri 10:19-25. Cifukwa ca zomwe Yesu anaticitira ife, tikhoza kupita kwa mpando wa cifumu ndi citsimikizo. Tidziwa Mulungu atikonda, sitiopa, Yesu sadzaphwanya pangano lace ndi ife. Iye ali okhulupirika.

CIKHULUPIRIRO, CIYEMBEKEZO NDI CIKONDI

Tiri ndi cikhulupiriro ndipo tikhoza kupita kumaso a Mulungu. Yesu, wansembe wathu, ayembekezera kutithandiza.

Tiyenera kugwirira ku ciyembekezere comwe tiri naco. Ici ndi ciyembekezo colimba kuti tidzakhala ndi Yesu muyaya. Tidzagawana naye ulemmerero.

Tiyenera kuganzira za njira ya kulimbikitsa abale ndi alongo mwa Kristu. Iyi ndi nthawi yathu ya kuonetsa cikondi comwe Mulungu anatipatsa. Titumikira ena mu njira zambiri, kuonetsa cikondi comwe tiri naco kwa iwo.

Ngakhale mu masiku oyamba a Cikristu, anthu ena aganiza kusiya kupita ku mapemphero. Mlembi wa Ahebri anawakumbutsa kuti ayenera kukomana pamodzi kuti athandizane wina ndi mzace. Werengani Ahebri 10:25 kaciwiri. Anthu acikristu ayenera kukomana pamodzi kupembeza. Pamene tikomana ndi okhulupirika ena, tilimbikitsana wina ndi mnzace.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Popeza tiri ndi moyo watsopano wacikhulupiriro ndi ciyembekezo, tiyenera kuthandiza ena. Tiyenera kulimbikitsana wina ndi mnzace. Tiyenera kugwirira pamodzi nchito zabwino.

Tiyenera kukomana pamodzi kupembedza Mulungu ndi zomwe iye acitira ena. Kukomana pamodzi munga Akristu cithandiza ife kudziwa Mulungu. Citithandiza kuzindikira kuti sitli tokha. Yesu ali nafe.

Ana a Israyeli anaiwala Mulungu. Kodi mwaiwala Mulungu? Anaphwanya lonjezo lao kwa Mulungu. Kodi mwaphwanya malonjezo anu kwa Mulungu. Ana a Israyeli ena anaiwala kukomana pamodzi munga Akristu. Kodi mwalephera kupembedza ndi Akristu ena ndi gawana nao cikondi ca Mulungu? Kodi muli kulimbikitsa ena mu cikhulupiriro cao? Kumbukirani kuti pamene muiwala Mulungu mucimwa. Yesu anafa kamodzi cifukwa ca macimo athu. Nsembe yopambana ija inakwanira kufikira muyaya, kwa anthu onse.

Cimo nthawi zonse siiyenda yokha. Cimo imodzi itsogolera kwa ina. Kuba kutsogolera kunama bodza.

3. 19:13-14. Kuyera kufunika munthu kusunga Malamulo. Ambuye anali kulankhulira anthu amve anali osauka ndipo ofoka. Kubera anthu omwe awagwirira nchito. Ndalama ziyenera kuperekedwa.

Kuyera kuletsa ife kunena zoipa pa munthu wina. Kapena kukhala osasamala.

4. 19:15-16. Kuonetsa kuweruza mucilungamo osanetsa sankho, kwa olemela ndi osauka. Kunena mau oipa kuletsedwa. Ngakhale mu bwalo la mlandu osamvetsera ku mau otere. Ngati bwalo la mlandu siili kuweruza mucilungamo, munga Akristu tidziwa kuti Mulungu adzapanga zonse kukhala bwino pamene adzabwera.

5. Kuyesa kunena bodza kuti tipate kuyera ndi cinthu comwe sicifunika.

6. 19:17-18. Lamulo lomaliza la kuyera ndi lodziwika kwambiri. “Konda mnansi wako munga uzikonda iwe wekha.” Ilankhula za mtima wa munthu pa mnansi wace.

Mu Levitiko 19:17 ndiponso mu Agalatiya 6:1, anthu a Mulungu auzidwa kuthandiza anansi ao pa kuwathandiza pamene alakwitsa. Muyenera kucita ici munjira yabwino, yofatsa. Pamene wina ali kucita coipa, ndipo si mumuza, ndiye kuti mugawana naye kulakwa kwace pamaso pa Mulungu.

Musabwezere pamene wina akucitirani coipa. Iyi ndi nchito ya Mulungu. Akristu ayenera kukhala oyera cifukwa Mulungu ndi woyera.

KUPHUNZITSA PHUNZILO

KUDZIWITSA

Nenani: “Mariya anali mzimai wabwino wa Cikristu amene anali kupita kumpingo nthawi nzonse. Pamene kunali nchito ku mpingo Mariya anali komweko kuthandiza. Ngati panali kalasi latsopano lomwe layambidwa, Mariya anaona kuti yakonzekeredwa. Anthu ambiri anamuyamika.

“Tsiku lina banja latsopano linabwera kumpingo. Mzimai wa banja limenelo, Estere, anali wokoma mtima kwambiri. Mariya anali m’modzi wa iwo amene anawaitana kunyumba kwace kukadya cakudya. Mariya anakonda Estere kwambiri ndipo anaganiza kuti akhale mtsogoleri wa azimai. Anamumva pamene iye anaimba conco anapempha abusa kuti akaimbe kumpingo.

“Pamene kunapita miyezi yambiri anthu anaona mphatso zambiri zomwe Estere anali nazo, ndipo anampempha kucita nchito zambiri zosiyana-siyana. Mariya anali wokondwa. Estere sanali wokondwa. Cinali kuonekeratu kuti ngakhale

MUTU 11

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Ndifuna ophunzira anga kugwiritsa nchito mutu 10 ndi 11 kukuthandizani kupita kuciyero.

ZOTHANDIZIRA PAKUPHUNZITSA: Lembani malamulo khumi mwacidule, pa bolodi kapena pa pepala lalikulu. Ikani pomwe ena akhoza kuiona.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Werengani Levitiko 19:2. Ncifukwa nciani Mulungu anapatsa munthu malamulo? Mu ndime iyi tipeza cifukwa. “Udzakhala oyera cifukwa ine Mbuye Mulungu wanu ndine Oyera.”

Tiyenera kumvetsetsa kuti Mulungu afuna amuna ndi akazi omwe ali olola kumvera iye kukhala ndi umoyo woyera. Mau awa analembedwa kwa ana a Israyeli kuwakumbutsa kuti maganizo ao anaonetsera momwe iwo analiri.

Ngati anthu amvera malamulo a Mulungu, adzakhala ndi khalidwe labwino. Kukhala oyera sikwapafupi. Koma ncofunikira kwambiri kuti Mulungu analankhulapo kwambiri mu Liu lakuti “*Ine ndine Yehova*,” Khumi ndi Kanai ali kunena tero. Ngati malamulo awa ndi ofunikira kwambiri kwa Mulungu, ndiye kuti anthu a Mulungu ayenera kumvera iye.

Levitiko 19:9-18 ikhoza kugawidwa mu magawo asanu aziphunzitso. Zonse zinena pa munthu ndi munthu mnzace, nchito yomwe malamulo a kuyera afuna munthu kucita.

1. 19:9-10 Kuyera kufuna kusamalira osauka. Mulungu ndi Mulungu wa osauka ndipo osowa. Anthu a Mulungu ndi adindo ace kunyamula malamulo ace. Mu khalidwe la Mkristu simuyenera kupezeka malo a kuzikonda.

Ana a Israyeli analondola lamulo limeneli pa kusiya mbali ya munda uli wonse wasagwiridwa. Colinga cinali cakuti asiye munda wa cisanu ndi cimodzi kwa osauka. Mu munda wa mpesa, anchito anali kutenga zokolola zoyamba. Zazing’ono zotsalazo zinafunika kutsala kwa osauka ndi osowa.

2. 19:11-12 Malamulo atatu anaikidwa mu ndime zimenezi. Mbali iyi ilankhula pa kuba ndi bodza

MUTU 3

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Yesu ndi pangano latsopano pakati pa Mulungu ndi anthu.

COLINGA: CAKUPHUNZITSA: Ndifuna ophunzira anga kuphunzira kuti pangano lakale pakati pa Mulungu ndi anthu inacotsedwa ndipo tsopano pali yatsopano ya Yesu.

ZOTHANDIZIRA PAKUPHUNZITSA: Ngati mukhoza, bweretsani kapepala pomwe anthu analemba kuonetsa kusunga pangano lao.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Mu Ahebri 8:7-13 Muli mau atali ocokera mu Yeremiya 31:31-34. Sungani ndime izi za mu cipangano cakale pafupi pamene muphunzira ndime za mu Ahebri. Yeremiya anakhoza kuona kuti pangano lakale silikanakhoza kugwira nchito. Panafunika yatsopano.

Mulungu anapanga mapangano akale atatu. Yoyamba inali ndi Nowa, ina ndi Abrahamu, ndipo inanso ndi mtundu wa Israyeli. Pangano lotsiliza imene inali pakati pa Mulungu ndi Israyeli ndilo pangano ananena Yeremiya kuti silizagwira nchito.

Mulungu analonjeza Israyeli zinthu zina ngati iwo akanamvera ndi kumutumikira. Pangano ili siinali pakati pa anthu ofanana, monga pangano la Davide ndi Yonatani. Koma inali monga yomwe Mfumu zinapanga pakati pa mitundu atangojetsa. Mulungu ananena kuti Israyeli adzakhala mtundu wansembe, ndipo Mulungu adzawalipira iwo. Indetu, anali atawalipira kale pakuwatulutsa mu Aigupto.

Ndime ya 7 inena kuti pangano ili siinali yabwino, koma comwe cinapangitsa ndi kusamvera kwa munthu, osati Mulungu. Conco, munthu anapangitsa kuti pangano latsopano ikhalepo.

Ndime 8 kufika ku 12 ndi mau a mu Yeremiya pali kusiyana pa mapangano awiri. Coyamba ikanakhala kwa nyumba ya Israyeli ndi mnyumba ya Yuda. Ici citanthauza kuti pangano. Latsopano ikanamanga kusiyana pa mtundu. Caciwiri pangano latsopano likanakhala la onse. Aliyense anali momwemo. Cinthu cosiyana cacitatu cinali cakuti ikanalembedwa pa mtima wa anthu osati mu buku. Ici cinatanthauza kuti anthu akanamvera Mulungu cifukwa anakonda, osati cifukwa anakakamizidwa kumvera.

Ndime 12 ndi ndime yabwino yomwe inena kuti Mulungu sadzakumbukira macimo athu.

Ndime 13 ibwereranso ku mau ali mu ndime 7 kuti pangano lakale linali losakwanira. Itionetsa pomwe inalephera. Silikhoza kugwiritsidwa nchito ndipo lakalamba lifunika kutaidwa.

Ahebri 10:19-25 itipatsa malangizo anai kwa Akristu. Mlembi atiuza kugwiritsa nchito cikhulupiriro cathu, kugwirira ku ciyembekezo cathu ndi kuonetsa cikondi cathu pa kulimbikitsana wina ndi mnzace. Langizo la cinai ndi kusaleka kukomana pamodzi ndi Akristu ena.

Ndime 19 kufikira ku 22 zinena kuti tiyenera kubwera mopanda mantha pamaso pa Mulungu cifukwa mwazi wa Yesu utipatsa cilimbitso. Yesu ndi njira ya Mulungu yatsopano. Njira yakale iyi inali ya kupereka nsembe ya nyama, nyama zinafa, koma Yesu ndi wamoyo. Pa kufika pamaso pa Mulungu, tipeza Yesu ali kutiyembekezera kuti tumikira monga wansembe. Mitima yathu ndi nzeru zathu zinayeretsedwa ndi mwazi wace.

Ciyembekezere comwe tiyenera kugwirira ndi cipulumutso. Ici ndico ciyembekezo comwe tiri naco kuti Mulungu adzaombola omwe akhulupirira mwa Yesu monga Mpulumutsi wao. Ciyembekezo cathu sicacabe monga anthu amaonetsera masiku onse.

Tiyenera kulimbikitsana wina ndi mnzace kupyolera mu cikondi ndi kucitira zabwino wina ndi mnzace. Mkristu sayenera kukondwera pamene wina abwerera kumbuyo. Koma, tiyenera kunyamula wakugwayo ndi kuwathandiza.

Mlembi wa Ahebri anazindikira kuti gulu loyamba la Akristu, ena anali kulephera kukomana pamodzi. Anawacenjeza kuti sayenera kulephera kucita ici, cifukwa ena anafuna cilimbitso ca wina pamodzi. Anawacenjeza kuti sayenera kulephera kucita ici, cifukwa ena nafuna cilimbitso ca wina kuti akule muuzimu. Mukatenga khala la moto ndi kuliika pa yokha, imazima. Ndi cimodzi-modzi ndi Mkristu, sakhoza kukula kopanda kukhala mu cijanano ndi ena.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Onetsani kalasi lanu pepala kapena pangano lolembedwa yomwe mwabweretsa. Fotokozani kuti ndi pangano pakati pa anthu awiri kapena opambana. Uzani kalasi kuti pangano ili tere (Anthu awiri akwatirana), wina agulitsa munda wace kwa wina, kapena wina abvomerezana kugwirira nchito wina kwa kanyengo.

KUKHALA UMOYO WABWINO MASIKU ONSE

Anthu a Mulungu anafunika kukhala okhulupirika mu kacitidwe kao konse. Bambo wina wa Cikristu anapita ku banki. Pamene anapatsidwa ndalama zomwe anali kufuna, anacoka kuti akawerenge ndalamazo. Anadabwa kwambiri! Panali K200.00 pamwamba. Anatenga ndalama zija ndi kupita nazo kwa bambo wa m'banki uja ndi kunena, "Mwandipatsa ndalama zambiri pamwamba kupambana zomwe ndinafunu."

Munthu uja anakondwa kwambiri kuona kuti ndalama zabwezedwa. Iye akanalipira ndalamazo kutha kwa tsiku pamene zikanawerengedwa. Akristu ayenera kukhala okhulupirika nthawi zonse.

Sitikhoza kukhala Akristu pa Sabata pokha. Cikhulupiriro cathu ca Cikristu ciyenera kuonetsedwa masiku onse. Mulungu atikonda ife. Tionetse cikondi cathu kwa Mulungu m'mene tikhallira. Tiyenera kukhala okhulupirika.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Akristu ayenera kuonetsa cilungamo kwa anthu onse. Mulungu aona munthu mosasiyanitsa cifukwa ndi woyera. Afuna ife kuti tikhale oyera. Afuna kuti tikhale monga Yesu.

Kodi muli okhulupirika mukacitidwe kanu? Kodi mumabela ena? Kodi mumanamiza akulu-akulu anchito anu? Kodi mumasunga malonjezo kwa anthu ena? Kodi mumanena bodza? Kodi mufunika kusintha umoyo wanu? Kodi mukumbukira phunziro la Mutu 10 m'buku ili? Mulungu ali nafe nthawi zonse. Atidziwa bwino. Sitikhoza kubisa kanthu kali konse kwa iye. Kodi muona bwanji umoyo wanu ku colinga ca Mulungu?

Mulungu afuna kuti munthu aonetse cikondi cace kwa Mulungu pa kukhala umoyo wabwino.

Munthu sakhoza kukhala woyera kopanda thandizo la Mulungu. Munthu afunika thandizo la Mulungu kumuthandiza. Mzimu Woyera omwe uli mwa iye upangitsa munthu kukhala ndi umoyo wangwiro pa maso pa Mulungu.

MALAMULO ENA A KUKHALA UMOYO WABWINO

Werengani Levitiko 19:9-18. Mulungu anadziwa kuti anthu adzafunika kuthandizana wina ndi mnzace. Mulungu anadziwa kuti munthu adzikonda kwambiri. Koma lamulo la Mulungu likali labwino. Malamulo ena a Mulungu ndi awa:

1. Ganizirani za anthu ena. Thandizani kudyesa osauka pa kusiya cakudya cina m'munda kuti akolole. Ngati muli ndi munda kololani cakudya cina ndi kuwapatsa.
2. Khalani okhulupirika. Musabele munthu. Ngati mulipilidwa malipilo a nchito yanu pa tsiku, gwirani nchito imeneyo. Musabele akulu a nchito yanu. Nenani coona.
3. Musanene bodza kuti ncoona. Ici cibweretsa manyazi pamaso pa Mulungu. Nthawi zonse nenani coona.
4. Musapange lonjezo la bodza. Ngati munena kuti mudzacita cinthu. Citani cimeneco. Sungani lonjezo lanu.
5. Khalani okhulupirika ndi anthu omwe agwira nchito ndi inu. Pamane Mulungu anapatsa lamulo lace, anthu anali kulandira malipiro a ang'ono kwambiri. Anali kulipilidwa masiku onse kuti apeze cakudya ca tsiku limenelo. Akulu a nchito ayenera kukhala okhulupirika ndi anthu omwe agwira nao nchito.
6. Khalani okoma mtima kwa anthu opunduka.
7. Citani cilungamo. Mulungu ananena kuti ali yense ayenera kupeza cilungamo mu nyumba ya malamulo. Mulungu ananena kuti anthu onse ayenera kupenyedwa cimodzi-modzi.
8. Musanene bodza. Mulungu afuna anthu ace kukondana wina ndi mnzace.
9. Konda mnansi wako monga udzikonda iwe wekha. Asungeni bwino.

Uzani anthu tanthauzo la paangano. Lankhulani za kufunikira kwace. Funsani kukalasi lanu ngati ena analowamo mu pangano. Tengani mphindi zazing'ono kuti alankhuzane.

Funsani: “Kodi ndani adzatiuza tanthauzo la liu lakuti “pangano”? Lolani ophunzira kuyankha.

KUMASULIRA

Ophunzira anu atsegule ku Ahebri 8:7-13. Auzeni apeze Yeremiya 31:31-34 nayonso. Uzani wina kuwerenga mutu umodzi mu Ahebri wina mu Yeremiya.

Funsani: “Kodi pangano loyamba ndi lotani? Wophunzira wina anene za pangano lakale. Gwiritsani nchito Genisis 12:1-3 kulankhuzana za pangano lakale.

Nenani: “Pangano la m'Cipangano Cakale inali mu malamulo ndi nsembe. Mkulu wansembe anali kulowa mu cipinda coyera atanyamula mwazi wa nyama kuti aperckere anthu nsembe. Tinalankhula za izi nthawi ija yomwe tinakomana. Posacedwa anthu anaiwala Mulungu. Anakana kumvera iye. Analephera kupereka nsembe zocotsa macimo. Kupitira mwa aneneri Mulungu anakakamiza anthu kubwerera kwa iye. Pamene zaka zinali kuyenda, alaliki naonso anali kulankhula kwambiri. Ndipo, Mulungu anapereka uthenga wapadera kwa Yeremiya. Pangano latsopano linafunika. Lakale linalephra.

Funsani: “Kodi ndi kusiyana kotani komwe muona mu pangano lakale ndi latsopano?” Lankhuzanani mu kalasi. Gwiritsani nchito kuphunzira koyamba kuti mupeze zofunikira.

Funsani: “Kodi wina wa inu akhoza kuwerenga Ahebri 10:19-25?”

Nenani: “Yesu ndi pangano lathu latsopano. Wansembe anafunika kulowa mu cipinda coyera kupita pa cinsaru comwe cinapatula Mulungu ndi anthu. Mnomfu wa kuthupi lace unagwira nchito monga nsaru, momwe Yesu anapitila kulowa mu cipinda coyera. Mnomfu wace unang'ambika pakati ndipo mwadzi wace unataika. Yesu analowa mu cipinda ca Mulungu atanyamula mwadzi wace, osati mwadzi wa nyama za kufa. Iye ndi njira ya moyo yatsopano ya kwa Mulungu.

“Yesu apanga cikhulupiriro cathu kukhala colimba. Mlembi wa Ahebri alimbisa Akristu kugwirira cikhulupiriro cao kwa Kristu. Ici ndi cikhulupiriro kuti tidzakhala muyaya ndi Mulungu. Ici sicikhulupiriro cacabe, koma coona.

“Tiyenera kukondana wina ndi mnzance ndi kulimbikitsana kukhala umoyo monga wa Kristu. Malo abwino akuti Mkristu akule ndi mu mpingo, koma Akristu oyamba aja anali atasiya kukomana pamodzi. Kodi pali mafunso pa ndime izi?” Yankhani ngati pali omwe afunsa.

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Nenani: “Yesu akhala pangano lathu latsopano. Ici citanthauza kuti akhala khomo la kwa Mulungu. Mu pangano latsopano, anthu onse a mtundu uli wonse akhoza kukhala colowa ca Mulungu. Pangano linalembedwa pa mtima wathu. Zoonadi Yesu walowa mu mtima mwathu momwe alamulira monga Mbuye. Iye akhala pa mpando mu mitima yathu, ndipo ife timamumvera.”

“Titumikira Mulungu wabwino. Iye ayesa nthawi zambiri kubweretsa anthu kwa iye yekha. Anakwaniritsa pamene Yesu anafa pamtanda.”

Pemphani gulu kutseka maso ao ndi kupemphera mwa cete kuyamika

Mulungu cifukwa ca nsembe ya Yesu kuti tikhale mu banja losankhidwa.

MUTU 11

MALAMULO A KUKHALA UMOYO WABWINO

COLINGA: Phunziro ili idzandithandiza kusankha kukhala woyera mu umoyo wanga.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Levitiko 19

NDIME ZA MPHUNZIRO YA LERO: Levitiko 19:2, 9-18

MAU APAMTIMA: “...*Udzakhala oyera, popeza ine Mbuye wako ndine woyera.*” (Levitiko 19:2)

Wacimishoni wina akumbukira pamene anali mwana wa mng’ono Anaganiza kuti anafunika kupita kwa amai ace ndi kuwauza kuti awakonda. Palibe kanthu pena anali kusowera kapena kugwira nchito. Iye akangoganiza anali kupita ndi kuwauza amai ace kuti “ndi kukondani.”

Amai ace anali kukondwa kwambiri pakumva mwana wao kuwauza tere. Ndi cimwemwe cinaturuka kukamwa kwao ndipo anakumbatira mwana uja.

Mulungu ali cimodzi-modzi. Amakonda kumva ife tiri kunena kuti timukonda. Mu buku iyi tamphunzira za cikondi ca Mulungu kwa anthu ace. Tinaphunzira momwe Mulungu anapitiliza kupatsa zinthu zabwino kwa munthu cikondi ici ncofunika kubwezera. Munthu amabwezera pa kacitidwe kace. Amayankha momwe amverera Mulungu.

Mphunziro lathu lero, tidzaphunzira za malamulo ena a Mulungu. Mayesero a ci Kristu coona ndi momwe tikhalira. Tiyenera kuika malamulo a Mulungu mu kacitidwe ka umoyo wathu. Tiyenera kubvomereza cikondi ca Mulungu.

CIFUKWA CACE CA KUKHALA NDI UMOYO WABWINO

Werengani Levitiko 19:2 “... *udzakhala oyera, cifukwa ine Mulungu wako ndine oyera.*”

“Kuyera” mu Cipangano Cakale cinatanthauza “kuikiza padera.” Pamene “kuyera” anena za Mulungu atanthauza kuti alibe cimo, ndipo ndi wangwiro. Mulungu alibe cimo. Ali oyera. Mulungu sali cimodzi-modzi ndi munthu. Mulungu ndi oyera.

Cifukwa Mulungu ndi Woyera, afuna anthu ace kukhala oyera. Anthu a Mulungu ayenera kuikizidwa padera ku zoipa za m’dziko. Cipangano Catsopano cinena kuti Akristu ayenera kukhala m’dziko koma si a dziko.

kumwamba. Koma Mulungu amamva mapemphero athu nthawi zonse. Ngati sitimamva kuti ali pafupi, ndi cifukwa cakuti tinacimwa ndipo cimo yacinjiriza Mulungu kwa ife. Ici cikhoza kupangitsa Mulungu kulephera kuyankha mapemphero athu, koma amamva. Amamva pamene tipempha cikhululukiro. Ndipo amabwezera ciyanjano cathu. Mulungu ali kuyembekezera kuti tibwerere kwa iye. Wina ananena kuti ngati simukhoza kumva kuti Mulungu ali pafupi ndi inu, ncifukwa cakuti inu munacokapo, osati Mulungu. Mu Mateyu 28:19-20, Mulungu alonjeza kuti adzakhala ndi ife nthawi zonse, ngakhale kumalekezera a dziko. Mulungu adzakhala komwe tikhala.”

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU:

Uzani ophunzira anu kutsegula mabuku ao kumalo komwe alemba kuti comwe citanthauza kwa ine? Pemphani wina kuwerenga mokweza.

Funsani: “Kodi kuli malo omwe simufunika kupita? Kumalo komwe Mulungu safuna inu kupitako? Kodi muli ndi abwenzi omwe Mulungu safuna kuti inu mukhale nao? Kodi muli ndi maganizo osakondweretsa Mulungu? Mulungu ali nafe nthawi zonse. Adziwa maganizo athu. Adziwa malankhulo athu tisanalankhule. Kodi kalankhulidwe kanu kakondweretsa Mulungu? Kodi mumafuna kubisala kwa iye?”

“Tiyeni tiganizire pa izi bwino-bwino. Tengani nthawi lero kuona zomwe zinacitika mu umoyo wanu sabata latha. Kodi mufuna kusintha umoyo wanu?”

Ophunzira anu agwetse nkhope zao. Apemphererani kuti atenge nthawi yao kuganizira mau awa, maganizo ndi kacitidwe. Pemphani Mulungu kuwapatsa cilimbitso kuti asinthe komwe afunika kuti akhale ndi umoyo wokondweretsa Mulungu.

MUTU 4

CIKHULUPIRIRO, COLIMBA NDIPO COONA

COLINGA: Phunziro ili idzaonjezera kumvetsetsa kwanga kuti Mulungu ayembekezera ine kupitiriza kukula mu mzimu.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Ahebri 11:1-12:29

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Ahebri 12:1-17

MAU APAMTIMA: “*Mukapirira kufikira kulangidwa Mulungu acitira inu monga ngati ana; pakuti mwana wanjani amene atate wace wosamlanga?*” (Ahebri 12:7)

Mphunzitsi anauza wophunzira wace, “Ndiri ndi cikhulupiriro mwa iwe.” Kodi mphunzitsi anatanthauza ciani? Cikhulupiriro citanthauza kukhala okhulupirira kwambiri mwa cinthu kapena mwa munthu. Ici citanthauza kuti mphunzitsi anali ndi cikhulupiriro cakuti ophunzira wace angathe kucita cinthu cabwino.

Kwa Mkristu, wokhulupirira woona mwa Yesu, cikhulupiriro citanthauza zambiri. Cikhulupiriro ndi kukhulupirira mwa Yesu, Mwana wa Mulungu. Tikhulupirira Yesu kutipulumutsa ife. Ici ndi ciyambi ca cikhulupiriro cathu ca Cikristu.

Cikhulupiriro cathu, ciyenera kukula. Ciyenera kuyamba kukula pamene titabadwa mwatsopano. Cimapitirirabe kukula kufikira titafa ndi kupita kukakhala ndi Mulungu.

COLINGA CACIKULU

Mu Ahebri 12:1, tikumbutsidwa kuti sitili tokha mu cikhulupiriro cathu mwa Mulungu. Mlembi atiuza mu ndime ya 11 za amuna ndi akazi omwe anakhulupirira mwa Mulungu. Anasautsidwa, ambiri anafa koma anakhalabe okhulupirika kwa Mulungu cifukwa ca cikhulupiriro cao.

Munthu aliyense yemwe analandira Yesu ali ndi colinga mu umoyo wace. Colinga cace ndi kukhala monga Yesu. Palibe colinga cina copambana comwe munthu akhoza kukhala naco.

Tidziwa kuti cimo itiletsa ife kufika ku colinga cathu ca moyo wathu. Tiyenera kubwala, kusiya kumbuyo cimo iliyonse yotiletsa kufika ku colinga cathu.

Ganizirani munthu wothamanga liwilo, ayamba kuthamanga, atanyamula cinthu colemera kwambiri. Posacedwa adzataya katundu uja pa kuona kuti uli

kumucedwetsa. Ndi cimodzi-modzi ndi Mkristu yemwe afuna kukhala monga Yesu koma sacotsa katundu wace. Ici sicotheka, tiyenera kutaya macimo mu umoyo wathu, kuti tikhale ndi umoyo monga wa Yesu.

YESU, CITSANZO CATHU

Mu Ahebri 12:2-3 tiwerenga kuti Yesu anadzipereka iye yekha kuti tipulumutsidwe. Sitikhoza kubvutika monga Yesu anacitira. Iye anatenga malo athu pamtanda.

Kutilanga kutithandiza kukula mucikhulupiriro. Kusauka mwa Yesu kucurukitsa cikhulupiriro cathu.

Iye ndi citsanzo cathu cangwiro. Anasauka cifukwa ca anthu oipa.

Tiwerenga mu Ahebri 12:5-11 kuti Akristu ndi ana a Mulungu. Liu ili mu Cigriki la kuti mwana wa mwamuna, siitanthauza mwana mng'ono itanthauza mwana mwamuna sswamkulu.

Mwana wamkulu amamvetsetsa malangizo atate wace. Cifukwa ife tiri ana, ana akulu a Mulungu, tidzamvetsetsa malangizo a Mulungu. Tidzamvetsetsa kufunikira kwathu kulangidwa, pamene tilephera kumvera Mulungu.

KULANGA KWACE KWA MULUNGU

“Kulanga” ndi kaphunzitsidwe kanzeru ndi khalidwe la munthu kuti abale kuziletsa ndi kumvera. Kulanga ndi kuphunzitsa.

Mulungu atikonda ife ndipo ayenera kutilanga kuti tikhale momwe tifunikira kukhalira. Cikondi cathu ndi ulemu kwa iye zikula pamene tilangidwa.

Pamene Mulungu aphunzitsa ana ace, cikhala cowawa. Koma mtsogolo mwace zotsatira zace ndi zabwino. Zotsatira zace ndi cilungamo, kuyera, kulola kumvera cifuniro ca Mulungu ndi colinga cace mu umoyo wathu, umoyo wabwino, kugwira nchito bwino, kukhala mu ciyanjano ndi Mulungu, kuledza mtima, cikhulupiriro, mtendere, cikondi ndi kufatsa.

Zotsatira zace za Mulungu ndi za muyaya. Tikhala ana oyera, tikhalanso omvera kwa Mulungu.

Koma pali ziopyezo za Mkristu zomwe amakomana nao pamene ayesa kukhala umoyo wokhulupirika. Mulungu amapatsa Mzimu wace kuthandiza pa nthawi ya mabvuto. Mu Ahebri 12:12-17, Akristu alimbikitsidwa kukula kuuzimu.

Ndi capafupi kwa Mkristu kukhala waulesi. Mkristu waulesi amasiya kuwerenga Buku Lopatulika lace. Amasiya kupita kawiri-kawiri kumpingo. Iye tsopano wakhala waulesi, ndipo sacitira umboni kwa ena monga afunikira kucitira.

Wolemba Masalmo apitiriza kunena kuti maganizo a Mulungu ndi abwino kwa iye. Maganizo amenewa ndi ambiri kwambiri kuti apambana zonse.

Ndime ya 19-24ndi pemphero lakuti oipa adzabvutika ndiponso kuti Mulungu adzasanthula mtima wa wolemba Masalmo. Oipa amenewa aoneka monga anali adani a Mulungu ndiponso a olemba Masalmo.

Mau mu ndime 23 ndi 24 ndi a kuzipereka kwa Mulungu. Atha kunena kuti Mulungu amudziwa mokwanira, apempha Mulungu kumusanthula kupeza coipa mwa iye. Sanafune ciri conse kumulesa kulowa mu njira ya Muyayaya

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Gwiritsani nchito nthano zomwe munatenga. Gawanani ndi ophunzira anu zinthu zomwe zinacitika kwa Akristu omwe anamva Mulungu ali kukhala pafupi ndi iwo. Tengani nthawi yaikulu kulankhuzana pa zinthu zimenezi kuti aphunzire zambiri kucokera kwa izi.

Mutatha kunena nthano zanu, pemphani ngati pali wina yemwe akhoza kugawana nanu nthano yofanana ndi yomwe mwanena.

Nenani: “Mulungu ali nafe nthawi zonse. Pamene tifuna thandizo kapena kufungatilidwa alipo kutipatsa. Phunziro lathu lero ndi la munthu pa kudziwa Mulungu kukhala pafupi ndi iye.”

KUMASULIRA

Uzani ophunzira anu kutsegula ku Salmo 13 ndipo alondole ndime pamene ziwerengedwa.

Kugwiritsa nchito mau ali pa kuphunzira koyamba monga cotsogolera, uzani kalasi kuti Salmo iyi ikhoza kuikidwa mu magawo anai. Masulirani gawo liri lonse. Funsani ngati kuli mafunso.

Funsani: “Kodi munayesapo kale kuthawa Mulungu?” Si cinthu capafupi. Akristu ife timadabwitsa nthawi zina. Pa sabata tikhoza kuimirira mu mpingo ndi kunena kuti Mulungu ali nafe. Tikhoza kupempha Mulungu kuti atsogolere umoyo wathu ndi kutionetsa cifuniro cace. Ndipo pa tsiku loyamba, tikhoza kuyamba kubisala iye cifukwa ca cimo lomwe tacita. Tifuna kuti iye akhale pafupi ndi ife, koma osati nthawi zonse. Tifuna kusankha nthawi ija yomwe tifuna. Koma Mulungu sali tero. Sitimuitana kuti abwere pafupi ndi ife. Iye alipo kale. Ali nafe usiku ndi usana ngakhale kuti sitimazindikira nthawi zina.

“Nthawi zina pamene tipemphera, sitikhoza kudziwa kuti Mulungu ali pafupi ndi ife. Tikhoza kumva monga kuti tiri tokha ndi kuti mapemphero athu safika

MUTU 10

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Mulungu adziwa zonse za munthu aliyense.

COLINGA CAKUPHUNZITSA: Ophunzira anga ayenera kumvetsetsa kuti Mulungu awadziwa mokwana.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Lankhulani kwa anthu 5-4) za nthawi yomwe anamva kuti Mulungu anali pafupi nao. Cingakhale cabwino kufunsa abusa. Mukhoza kuthandiza anthu pamene munena tere, “Kodi pali nthawi yomwe munamva kuti Mulungu ali pafupi ndi inu kwambiri? Pena inali pa nthawi yomwe munali ndi mabvuto monga imfa kapena matenda. Kapena pamene cinthu cabwino kwambiri cinacitika, monga kucira kwa matenda, kubadwa kwa mwana ndi zinthu zina. “Lembani pa cipepala zinthu izi kuti mutapita kukalasi mukalankhule nao.”

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Salmo 139 ndi Salmo yabwino. Wolembe Masalmo anali atakomana ndi Mulungu, kotero kuti anafuna owerenga ace kutero naonso. Kwa iye Mulungu sanali kutali, anali pafupi. Mulungu anadziwa munthu uyu ngakhale m'mimba pamene anali m'mimba. Anamdziwa asanabadwe. Anadziwa kuti Mulungu anali pafupi nthawi zonse. Kulibe kanthu ndi komwe anapita cifukwa nakonso Mulungu analiko.

Salmo iyi ikhoza kuikidwa mu zigawo zinai, Ili yonse ndi mutu wosiyana. Ndime 1-6, 7-12, 13-18 ndi 19-24. Tidzaphunzira mbali ili yonse pa yokha.

Ndime 1-6 itiuza kuti Mulungu adziwa zonse. Anadziwa wolembe Masalmo cifukwa anamusanthula ndi kumudziwa. Anadziwa pamene iye anakhala ndi kudya. Mulungu anadziwa maganizo ace. Mulungu ali ndi nzeru za masiku a munthu. Anamuzungulira iye. Cimene anatanthauza ndi cakuti Mulungu anamtsogolera kutsogolo kwace. Anadabwa kuti Mulungu anadziwa zambiri za iye.

Ndime 7-12 itiuza kuti Mulungu ali pali ponse. Wolembe anafunsa komwe akanathawira kubisala Mulungu. Kuli konse kumene iye anapita Mulungu anali komweko. Ngati iye alowa m'manda, Mulungu ali komweko. Akuti ngakhale mdima siukhoza kumuphimba iye kwa Mulungu.

Ndime ya 13-18 litiuza kuti Mulungu ndi mlengi wathu. Adziwa mathupi athu kupambana ife eni ace. Anatidziwa ngakhale tisanabadwe.

Akristu ayenera kupenyetsetsa pa ciopyezo ici ngati iwo aona kuti ayamba kukhala aulesi, ayenera kulapa ndi kupempha Mulungu kuwathandiza.

Mulungu amalenga ana ace kuti amvere iye. Ndipo adzafuna kugawana cikondi ca Mulungu ndi ena. Ana a Mulungu amagawana wina ndi mnzace mu cikhulupiriro cao.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Mkristu aliyense afunika cikhulupiriro cacikulu. Pamene tigwiritsa nchito cikhulupiriro cimene tiri naco, cimakula. Kodi timagwiritsa motani cikhulupiriro cathu?

Ganizirani za wina yemwe sali Mkristu. Mufuna kuti munthu uja akhale Mkristu. Muganiza kuti muli ndi cikhulupiriro cacing'ono. Muganiza kuyesa kugwiritsa nchito cikhulupiriro comwe muli naco kuti mubweretse munthu uja kwa Kristu. Muli a mantha, koma mudziwa kuti mukhoza kupemphera. Mupemphera, “Ambuye, lolani kuti ine ndionane ndi munthu uja wotaika.” Mulungu ayankha pemphero, ndipo muonana ndi munthu wotaika uja. Pena mudzakhala a mantha kulankulana naye.

Usiku uja mukumbukira momwe Mulungu anayakhira mapemphero lanu. Ndipo mulimbikitsidwa ndi kuyamba kupemphera. Conco mupemphera “Ambuye, zikomo pa kunditsogolera kwa munthu wotaika mawa ndiloleni ndikakomanenso naye, ndipo ndipatseni cilimbitso kumuza kuti ndine Mkristu.”

Ambuye adzayankhanso pemphero imeneyo. Muli kugwiritsa cikhulupiriro comwe muli naco, ndipo muli kukula. Ngati mupitiliza mu njira imeneyi, Mulungu adzakuthandizani kukuonetsani munthu wotaika momwe akhoza kukhalira Mkristu.

Mkristu aliyense ayenera kukhala ndi colinga ca umoyo wace. Colinga cimeneci ciyenera kukhala monga Kristu masiku onse. Pa kufika ku colinga cimeneci kufunika kumvera. Adzatithandiza kukula mu cikhulupiriro coona.

Kodi muli olola kulangizidwa mu umoyo wanu?

MUTU 4

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Mulungu ayembekezera wokhulupirira aliyense kukula muuzimu.

COLINGA CAKUPHUNZITSA: Ndifuna ophunzira anga kumvetsetsa kuti kukula muuzimu citanthauza ciani. Phunziro ili lidzawapatsa zocita zina kuwathandiza mu kukula kwao kwa uzimu.

ZOTHANDIZIRA PAKUPHUNZITSA: Pepala lokwanira ndi colembera kwa ophunzira aliyense. Bolodi kapena pepala lalikulu.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Ahebri 12:1-17 ndi ndime zomwe ziphunzitsa za cikhulupiriro colimba ndipo coona.

Mu ndime yoyamba, mlembi wa Ahebri anena kuti Akristu ali ozungululidwa ndi mboni zambiri, ali ambiri monga thambo. Thambo ili la mboni ndi Akristu mu ndime 11 ndi Akristu ena omwe anakhala padziko lapansi. Awa anthu alipo cifukwa ca zolinga zambiri. Iwo afunika kuyang'anira kuona kuti tifika ku colinga cathu. Iwo ananyamula cikhulupiriro kwa kamtunda. Tsopano afuna kuona momwe tinyamulira kwa mtunda omwe tifunika kuthamanga. Ali komweko kulimbikitsa amene ali kuthamanga.

Liwilo lomwe Mkristu ayenera kuthamanga, ayenera kuthamanga bwino. Cimo liri lonse liyenera kusiyidwa kuti acite bwino. "Cimo lomwe ligwilira pafupi" linaonetsa cithunzi-thunzi ca wothamanga pamene aika cobvala cace cacitali pansi kuti athamange bwino. Cimo iyi ikhoza kuoneka ngati ka cimo kakang'ono poyamba, koma kakhoza kutiletsa kuthawa bwino.

Ndime ya 2 itiuza kuti tisayang'ane pa mtambo wa mboni ndi kuyesa kucita zomwe ali kucita. M'malo mwace maso athu ayenera kuyang'ana pa Yesu Kristu yemwe akhoza kuthamanga liwiro langwiro. Yesu uyu ndi yemwe anabvutika imfa ya pamtanda, imfa yopatsa manyazi. Mu maiko ena lero, imfa yopatsa munthu manyazi ndi kunyongedwa. Mu nthawi yomwe Yesu anali padziko lapansi, imfa yopatsa manyazi, anasungila mbala, inali imfa ya pamtanda. Yesu sanadandaule koma anali kuyang'ana ku cikondwerero comwe anali kubweretsa kwa Akristu ambiri omwe anapulumutsidwa cifukwa ca imfa yace.

Ndime ya 3 itiuza kuika maso athu pa iye, tiyenera kukhala monga iye anakhalira. Yesu anabvutika molimba mtima kuti nafenso tisalefuke ndi kugwa mjira kopanda kutsiliza liwiro lathu. Timayesa, koma palibe wina wa ife amene

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Kodi muganiza kuti ncabwino kuti Mulungu akukondani? inde! Kodi muganiza kuti ncabwino kuti Mulungu adziwa maganizo athu? Pena ganizo ili likupangitsani kwina ndi kuganiza. Ena a ife tifunika kusuka maganizo athu. Kodi ndi malo ati omwe mumakonda kupita kukaceza? Kodi ndi malo omwe Mulungu akhoza kukondwa kukuonani? Kapena mufunika kusintha zisankho zomwe mwakhala muli kupanga komwe mwagwiritsa nthawi yanu.

Kodi abwenzi anu ndani? Kodi mumatenga nthawi yanu ndi yani? Kodi muli okondwa kuti Mulungu akuonani ndi abwenzi anu amenewo? Kodi mufuna kusintha abwenzi ?

Kodi mumalankhula zotani? Kodi mumalankhula za nchito yanu, ndalama, moyo wanu, abwenzi kapena Mulungu wanu? Kodi mufunika kusintha zomwe mumakonda kulankhula? Ambiri aife tifunika kutero.

Kodi tikhoza kunena kuti, "Ndisanthuleni Mulungu ndi kudziwa mtima wanga! ndiyeseni ndi kudziwa maganizo anga."

Mulungu adziwa maganizo athu. Adziwa malingaliro athu. Adziwa zonse za ife. Iye ali pafupi ndipo oyembekezera kutithandiza. Mulungu afuna kuti timumvere. Afuna kuti ife tikhale ndi maganizo abwino ndi miyoyo yoyera. Afuna kuti timukonde ndi kumuyamika.

Kodi mufunika kusintha mbali ina ya umoyo wanu?

Mulungu adziwa zomwe tiganiza, ndipo adziwa zomwe tidzanena ngakhale tisanalankhule. Mulungu adziwa zonse. Tikhoza kumuza maganizo athu onse, ndi mabvuto.

Sitifunika kuelekeza. Iye adziwa kale momwe tiliri. Adziwa ngati ndiye aakulu kapena ang'ono. Ngati tidziwa kuti Mulungu adziwa zonse, tiyenera kuzindikira kuti ndi cofunikira kumvera iye.

MULUNGU ALI PALI PONSE

Pamene munali ana, kodi munacita cinthu coipa ndi kuyesa kubisa ku makolo anu? Pena munakwaniritsa kwa kanthawi. Koma sitikhoza kubisa kwa Mulungu. Ngakhale komwe timapita, ali komweko.

Mulungu atitsogolera. Atitetedza ku coipa. Afuna kutitetedza ndi kutilimbisa. Afuna kuti timumvera.

MULUNGU ANATIDZIWA TISANABADWE

Pamene musanabadwe, Mulungu anadziwa mbali ili yonse ya thupi lanu. Ndiye anapanga thupi lanu pamene munali mu mimba ya amai anu. Pfupa ili yonse, ciwalo ciri conse, ndi mbali yonse ya thupi lanu ili yodziwidwa ndi Mulungu.

Pamene munali kuyembekezedwa kubadwa, Mulungu anadziwa masiku onse omwe mudzakhala. Anapanga colinga ca umoyo wanu. Wolemba Masalmo anadabwitsidwa ndi nzeru izi kuti anauza Mulungu kuti nzeru zace zodabwitsa.

YAMIKANI MULUNGU CIFUKWA CA IYE

Kodi ndi liti pamene munayamika Mulungu cifukwa ca citetedzo cace? Tiri ndi zinthu zambiri zomwe tiyenera kutamanda Mulungu. Sikukhoza kukhala kukolola cimanga ngati kulibe dzuwa ndi mvula. Munthu alibe mphamvu padzuwa ndi mwezi. Mulungu alinayo. Tiyenera kumuyamika cifukwa ca zinthu zambiri zomwe amaticitira.

Ndi cobvuta kumvetsetsa momwe anthu apitiliza kukhala adani ndi Mulungu. Mulungu anaticitira zinthu zambiri kwa munthu. Koma wolemba ma Salmo ananena kuti adani a Mulungu ndi adani acenso.

NDISANTHURENI MULUNGU, NDI KUDZIWA MTIMA WANGA

Wolemba Masalmo anafuna Mulungu kuyesa mtima wace ndi maganizo ace. Sanafune coipa ciri conse mu mtima mwace. Sanafune ciri conse kuimilira pakati pa iye ndi Mulungu. Anafuna Mulungu kumutsogolera muyaya.

adzapacikidwa cifukwa ca macimo a anthu, Yesu anacita. Akristu ambiri sadzafa cifukwa ca cikhulupiriro cao. Ena anafa ndipo enanso adzafa, koma si ambiri. Mlembi pena anali kukonzekera owerenga ace kubwera kwa mazunzo kuti ambiri adzafa.

Ndine ya 5-11 atiiza za kuzisunga kwa Akristu, Atate athu a padziko lapansi amalanga ana ao, Atate athu akumwamba amalanga ana ace. Ngati tikungosiyidwa tere, ndiye kuti aona kuti tiribe nchito. Kuphunzitsidwa kwathu kupita kutsogolo. Cingakhale cowawa pa nthawi ino, koma zotsatira zace zidzakhala zabwino kwa ife.

Ndime ya 12:17 itipatsa malangizo. Tiyenera kuzinyamula ife tokha. Ngati tikungokugwa, mtsogolo sitidzakwanitsa kuyenda bwino.

Langizo lina ndi kuyesa uku sikungokamba cabe. Koma, cithunzi-thunzi ndi ca munthu alikuyesa kwambiri kotero kuti thupi lace liri kuonetsa.

Langizo lacitatu ndi kuyesa kukhala oyera, kuyera ndi kuikidwa padera ku nchito ya Mulungu. Tiyenera kukula nthawi zonse. (monga Kristu) Kuti Mulungu atigwiritse nchito.

Langizo la cinai ndi kupenya mizu la kuwawa yomwe ikhoza kukula ndi kutibvuta. Ndime zonena za Esau zionetsa kuti Esau sanaika nzeru zace ku mphamvu ya kubadwa ngakhale pamene atagulitsa. Mtsogolo pamene analephera kutenga mphamvu yace, ngakhale analira sanakhoze kutero.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO ILI

KUDZIWITSA

Nenani: “Wina anena kuti anthu okwanira 440 adzathawa liwiro posacedwa. Iye auza othamanga liwiro kuzikonzekera iwo okha. Anthu ayamba kuzikonzekera. Ena athawira kwina ndi kuyesa. Ena amanga nsapato zao. Pamene mphindi ziri kuyandikira othamanga aja ayamba kucotsa zobvala zao.

“Tsopano liwiro loyamba, ndipo onse akonzekera kuti adzapambana. Iwo anaphunzira bwino ndi kuyesa masiku onse. Anthu awa anazipereka iwo okha ku nchito imeneyi. Aliyense anayembekezera kupambana.

KUMASULIRA

Nenani: “Monga anthu anali kuthamanga liwiro mu 440, naifenso tiri kuthamanga. Ena a ife tiri kuthamanga bwino: Ena ali kumbuyo ndipo ali kugwa. Akristu ayenera kudziwa kuthamanga bwino monga momwe amadziwira zinthu zomwe afuna kucita bwino. Tiyeni tiwerenge mau a lero ndi kuona zomwe mlembi anena za anthu othamanga liwiro.”

Uzani ophunzira anu kutsegula mabuku ao ku Ahebri 12:1-17. Werengani ndime yoyamba, ndipo gwiritsani kuphunzira koyamba kumasulira ndime. Pemphani ophunzira kuonjeza zomwe adziwa kapena funsani funso liri lonse pa ndime izi, lankhulani maka-maka pa cimo yomwe imagwirira pafupi. Chulani macimo ena omwe tikhoza kukhala nao monga ulesi, ukali, kutonza kusakhulukira.

Pitirizani mu njira imeneyi, kulankhuzana pa ndime ndi ndime kufikira 5-11, 12-17. Ziwani kuti ophunzira anu apatsidwa nthawi kuti aonjeze zofunikira. Muli kuphunzitsa akulu-akulu, ndipo nthawi zambiri zomwe akhoza kunena ndi zofunikira.

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Nenani: "Ndime 14 itiuza kuti tiyenera kuyesa kufika pa mtendere ndi kuyera. Kuyera ndi kukhala monga Yesu. Monga Akristu ici ndico colinga cathu, kukhala monga Yesu. Ngati tithamanga bwino, kuika maso athu pa Yesu, tidzakhala monga iye masiku onse lero, tiyeni tilankhule za njira zomwe tikhoza kukhala monga Yesu."

Patsani aliyense pepala ndi colemba. Nenani: "Tidzalankhuzana zinthu izi. Ndidzalembe pa bolodi zomwe mudziwa kuti zikhoza kuthandiza ife kukhala monga Yesu. Lembani pa mapapala anu. Mukhoza kuika pomwe onse akhoza kuona masiku onse. Mu njira imeneyi mukhoza kuonjeza maganizo ena nthawi zambiri, ndipo lankhuzanani ndi atsogoleri mu magulu, ndi kuona kuti zithandiza kukula muuzimu. Onetsetsani kuti zidzathandiza Mkristu kukula ku mau.

1. Pitani kumapemphero nthawi zonse.
2. Werengani Buku Lopatulika masiku onse.
3. Pempherani nthawi zonse (musanadye, musanagone, pa nthawi ya cete).
4. Uzani ena zomwe Yesu akucitirani.
5. Zikonzekereni inu nokha momwe angakhalire Akristu. Mukhoza kugwiritsa Aroma 3:23, 6:23; Yohane 3:16; Aroma 10:9-10.
6. Phunzirani kukhululukira ena pamene acita coipa kwa inu.
7. Citani cinthu cabwino kwa wina. Yesani kucita ici kopanda iye kudziwa kuti ndinu mwacita.

MUTU 10

MAONEKEDWE A MULUNGU NDI MUNTHU

COLINGA: Kodi Mulungu andiziwa motani? Phunziro ili idzandiuza.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Salmo 139

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Salmo 139

MAU APAMTIMA: "Ndidzapita kuti kuzembera mzimu wanu? Kapena ndidzathawira kuti kuzembera nkhoze yanu?" (Salmo 139:7)

Mwana wa m'ng'ono anali kusowera kunja kwa nyumba ya amai ace. Anali atatola tumitengo. Anafuna kupanga khola la "Nyama zace."

Pamene anagwira mtengo umodzi, analira ndi kutaya mtengo uja. Cifukwa unali ndi minga. Anali atalatsidwa ndipo mwazi unali kukha. Anatembenuka ndi kuyamba kuthamanga kwa amai ace misozi ili mumasaya. Azimai amadziwa zocita kuthandiza mwana pamene afunika thandizo.

Ana amapita kwa amai ao pamene ataphwetekedwa ndi pamene afuna thandizo. Kodi akulu-akulu amapita kuti? Ngati tipita kwa abwenzi kapena acibale, nthawi zina sadzamvetsa. Nthawi zina sathandiza. Pali wina, yemwe akhoza kuthandiza. Nthawi zonse amamvetsetsa. Ndiye Mulungu.

Mu phunziro la lero, tiphunzira kuti Mulungu analonjeza kukhala ndi anthu. Wolembe Masalmo anathawira kwa Mulungu pamene anafuna thandizo. Anadziwa kuti Mulungu adzamvetsetsa. Anadziwa kuti Mulungu anamkonda iye ndipo anali pafupi.

MULUNGU ADZIWA ZONSE ZA IFE

Werengani Salmo 139. Kodi munamvapo wina ali kunena, "Bwerani palibe ali kuona!" Kodi munamva ngati wina ali kuyang'ana? Munadziwa cifukwa wina anali kukuonani. Mulungu nthawi zonse ali kukuonani.

Nthawi zambiri tiwala kuti Mulungu adziwa zonse za ife. Yesu ananena kuti ngakhale tsitsi la kumutu kwanu anaiwerenga. Mulungu adziwa zonse za ife.

Mnyamata wina anati, "ndinayesa kuthawa kucoka kwa Mulungu, monga momwe Yona anacitira. Koma konse kumene ndinapita, Mulungu anali komweko. Wolembe Salmo 139 ananena cimodzi-modzi. Sitikhoza kusowa kwa Mulungu. Amadziwa komwe tiri ndi zomwe ticita.

kuyelekeza kutsogolera munthu kwa Kristu, ndidzayamba ndi kupempha umodzi wa ife kubwera ndi kukhala patsogolo pa gulu ndi kuyelekeza kukhala wotaika.

Onani kuti munthu yemwe mwasankha kusowera sowero ndi Mkristu. Mukhoza kulakwisa ngati musankha munthu wosakhulupirira.)

Gwiritsani nchito njira yomwe mudziwa yaifupi yobweretsa wina kwa Ambuye, yambani pa kulankhula za nchito yace, banja, nyumba. Tsopano pitani ku funso. “Kodi munalandira Yesu monga Mpulumutsi wanu?” Gwiritsani nchito Buku Lopatulika kuonetsa munthu ‘Wotaika’ Kuli anthu onse anacimwa ndipo afunika kupulumutsidwa. Kuti onse ayenera kulapa ndi kulandira Yesu. Ndipo aliyense ayenera kuuza ena kuti analandira Yesu. Mukhoza kugwiritsa Aroma 6:23, Aroma 3:23, Aroma 10:9-10 pa sowero lanu. Ena awiri abwere patsogolo ndi kucita cimodzi modzi. Pitolizani ngati muli ndi nthawi.

8. Perekani cakhumi ku mpingo.

9. Perekani zopereka zina ngati mukhoza.

10. Patsani abusa anu cakudya.

11. Cezerani wina amene alibe bwenzi.

12. Phunzirani kuyamikira. Yamikani Mulungu cifukwa ca cilengedwe cace, ndi zina zomwe muyenera kumuyamika.

Mutatsiriza mundandanda wanu, mukhoza kutseka ndi pemphero. Pemphani Mulungu kulola ophunzira kuyamba kuyesa kukhala monga Kristu.

MUTU 5

UMOYO WA CIGONJETSO

COLINGA: Phunziro ili idzandiphunzitsa cifukwa cace ndiyenera kukhala ndi cikhulupiriro colimba ca Mulungu.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Ahebri 13:1-25; 1 Akorinto 15:58

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Ahebri 13:1-8, 20-21

MAU APAMTIMA: *"Yesu Kristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi ku nthawi zonse."* (Ahebri 13:8)

Mtsikana wa mng'ono analandiridwa pa sukulu la a Baptist. Atate wace anaganiza kuti kunali nyumba yogonamo ya ana a akazi.

Iwo anafika pa sukulu imeneyo pa Sabata m'madzulo. Iwo anadabwa ndipo anakhumudwitsidwa pa kudziwa kuti panalibe nyumba yogonamo ya ana akazi.

Akulu a pa sukulu anatumia lamyi kwa abusa kuwauza za mwanayo. Anafunsa abusa ngati iwo anadziwa za banja la Cibaptist lomwe likanakhoza kusunga mtsikana. Abusa anaitana akulu a pa sukulu, bambo uja ndi mtsikana wao kunyumba.

Abusa ananena kuti akazi ao adzasunga mtsikana uja. Adzamsunga monga mwana wao. Bambo uja anadabwa kwambiri, cifukwa mtundu wao ndi mtundu wa abusa unali utakhala pa udani kwa zaka zambiri.

Cifukwa ca cikhulupiriro cao mwa Yesu, abusa anali ndi cigonjetso pa udani wa mtundu. Iwo pamodzi ndi mkazi ao anaonetsa cikondi cacikulu kwa iye kuti anali okonedwa pa zaka zomwe anakhala nao.

Naifenso tikhoza kukhala ndi umoyo wa cigonjetso. Ngati Yesu akhala mwa ife timakhala omvera kwa iye, tidzakhala ndi cigonjetso.

KONDANI AKRISTU ENA

Werengani Ahebri 13:1-8. Kukhala ndi umoyo wacigonjetso, Akristu ayenera kukondana wina ndi mnzace. Ngati Mkristu anena kuti akonda Mulungu koma sakonda Akristu ena, ali kunena bodza. "Munthu akati, kuti, ndikonda Mulungu, nadana naye mbale wace, ali wabodza: Pakuti iye wosakonda mbale wace amene amuona, sakhoza kukonda Mulungu amene sanamuona," (1 Yohane 4:20).

KUMASULIRA

Uzani ophunzira anu kutsegula mu Yesaya 55:1-9. Itanani wina kuwerenga ndime izi ku kalasi lanu.

Funsani: "Kodi ana a Israyeli anali kuti pamene mau awa analankhulidwa?" Kalasi lanu likhoza kudziwa yankho. (Anali ku Babulo.)

Nenani: "Ndiloleni ndi kupatseni mbiri ya ndime zimenezi. Ana a Israyeli analowa mu ciyanjano ndi Mulungu ataturuka mu Aigupto ndi Mose. Analonjeza kuti adzamvera Mulungu. Analephera kucita zomwe analonjeza. Mulungu anatumiza aneneri ndi athenga kukumbutsa anthu za pangano lao. Iwo anakana kumvera. Mmalo mogawana Mulungu ndi anthu ena, iwo anazipatula kwa anthu owazungulira.

"Potsiriza, Mulungu analanga anthu ace. Analola maufumu ena kulowa ndi kugonjetsa anthu ace osankhidwa. Analola adani awo kuwatenga kuukapolo.

"Poyamba, ayuda analira muukapolo muja. Iwo analira cifukwa sanakhoza kubwerera ku dziko lao. Koma zinthu zinayamba kukhala bwino. Ena a iwo anapatsidwa malo. Anayamba malonda. Anayamba kudiyera mu Babulo. Anakonda anthu aku Babulo. Anaiwala cifuniro cao ca kubwerera ku Yerusalemu. Iwo anali atakhala mu Babulo zaka 50. Kunali kutakhala ngati kwao tsopano.

"Mneneri anadza kwa iwo, kuwakakamiza kubwerera ku Yerusalemu. Cilolezo cinapatsidwa kwa iwo. Koma sanafune kupita. Ulendo wao unali wautali ndipo obvutitsa. Iwo sanafune kusiya zonse zomwe anali nazo ndi kupita ku dziko lomwe anali ataiwala. Awa ndi mau acidule a kumasulira cifukwa cace mau awa analembedwa. Ndani yemwe anafuna kusiya zinthu zonse zomwe anali nazo.

Funsani: "Kodi nciani cina comwe mneneri anawauza kucita? (Anafuna kudziwa ngati anaiwala cifuniro cace.)

Nenani: "Mneneri anawakumbutsa kuti Mulungu anali kuwayembekezera kubwerera kwa iye. Iye adzapitiriza kuwakonda monga mwa nthawi zonse anawacenjeza kuti sadzawayembekera muyaya. Iwo anafunika kuitana kwa Mulungu. Mulungu akanawakhululukira macimo ao. Anawauza kuti njira zace ndi nzeru zace zipambana zao."

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Nenani: "Mulungu akali kutikonda ife lero. Afuna yense wa ife kutero kulandira mwana wace. Sicolinga cace kuti tikabvutike. "Ndifuna kuti titenge nthawi lero,

Sakuswa lonjezo lace, koma aitana anthu kubwera kwa iye. Akhoza kuwalanga iwo. Iye safuna kucita ici. Conco aitananso Ayuda kuti alape.

Mu Yesaya 55:6-7 itiuza nyengo yomwe Mulungu adzaitana munthu kulapa. Palibe yemwe adziwa nthawi yace. "Funani-funani Yehova pamene apezeka" ndi uthenga womveka bwino. "Oipa ndi anthu omwe acita macimo poyera. "Osalungama" ndi anthu omwe acimwa m'maganizo ndi malo obisika. Zonse zidziwika kwa Mulungu. Onse aitanidwa kuti alape. Onse ndi ocimwa pamaso pa Mulungu.

Mulungu adzakhululukira onse amene alapa ndi kubwerera kwa iye.

Yesaya 55:8-9 anena kuti maganizo a Mulungu simaganizo athu. Kacitidwe ka munthu sikafanana ndi ka Mulungu. Masiku ano munthu amene afuna mtendere kupambana nkondo amuona kuti ali "wofoka." Mulungu sakwiya msanga. atiitananso kuyesa kubweza anthu kulapa ndi kubwerera kwa iye.

Samueli wa ciwiri 7:8-16 ndi mau a pangano la Mulungu ndi Davide. Analonjeza Davide kuti ana ace sadzacoka mu mbadwo wace. Mau awa Davide anaudzidwa ndi Natani kuti sadzaloledwa kupanga nyumba ya Mulungu. Koma Mulungu adzalola iye kupanga mndandanda wa mbandwo wa ana ace omwe udzindikiridwa ndi Mesiya. Mulungu anatsimikizira Davide mu ndime ya 15 kuti sadzacotsa cikondi cace kwa ana ace.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Pemphani ophunzira anu kutsegula mabuku ao ku Salmo 136. Auzeni kumasulira comwe cikondi ca Mulungu citanthauza. Atsogolereni kusiriza kuti cikondi ca Mulungu sicikutha. Palibe comwe tikhoza kucita comwe cikhoza kucosa cikondi ca Mulungu kwa ife. Sitiyenera kukhala "abwino" kulandira cikondi cace. Ciripo nthawi zonse, mu nthawi zabwino ndi zoipa. Ciri pomwepo pamene tikhala umoyo wa cigonjetso, ndipo ciripo pamene tiri ofoka.

Onani kuti onse ali ndi Mabuku Opatulika ofanana. Ndipo fotokozani; "ndidzawerenga mbali yoyamba ya ndime," Yamikani Yehova cifukwa ndi wabwino. "Ndipo ndifuna kuti nonse inu kuwerenga "Cikondi cace nca muyaya, 'ndidzawerenga "Yamikani Mulungu wa Milungu." Ndipo mudzawerenga pamodzi. Cifukwa cikondi cace nca muyaya "Tidzawerenga Salmo yonse motere,"

Tsopano werengani monga momwe mwafotokozera. Ngati mulakwisa poyamba, yambaninsu, kufikira mutakhoza kuwerenga Salmo yonse.

Ndipo nenani: Phunziro lathu litiuza kuti cikondi ca Mulungu ciri ndi ife nthawi zonse.

Kulibe kanthu ku mtundu komwe acokera. Ngati iye ndi Mkristu, ndi mbale wathu. Lero Akristu ayenera kuonetsa cikondi kwa wina ndi mizace.

Pamene buku la Ahebri linalembedwa, nyumba zosungiramo alendo zinali zoipa kwambiri. Akristu anathandiza ena pa kuwapatsa cakudya ndi malo ogonamo.

Masiku ano mu Africa, tikhoza kulandira abale a Cikristu. Tikhoza kucezera odwala muzipatala. Tikhoza kuwathandiza kuwagulira zinthu, tikhoza kuwathandiza kulela ana pamene wina adwala. Tikhoza kuthandiza mnansi wathu kulima.

Pali njira zambiri zothandiziramo anthu amene ali ndi zosowa.

PANGANI NYUMBA ZA CIKRISTU

Mulungu atiphunzitsa kuti tikhale okhulupirika kwa munthu yemwe tinakwatira. Ciribe kanthu ngati cikwati ndi ca mtundu, kapena ca Cikristu. Colinga ca Mulungu ndi mwamuna m'modzi kukwatira mkazi m'modzi kufikira imfa.

Kristu amatithandiza ife kukhala ndi nyumba za Cikristu zodzala ndi cikondi, malangizo, ndi pemphero. Atithandiza kukhala okhulupirika kuti cikondi cikule m'nyumba. Kukhulupirira wina ndi mizace ndi kukondana cimanga nyumba zolimba.

KHALANI OKONDWA NDI ZOMWE MULI NAZO

Ahebri 13:5 auza Akristu kukhutira ndi zomwe ali nazo. Sanena kuti Mkristu safunika kukhala ndi katundu. Iye akuti tiyenera kugwira nchito molimba kuti tipeze zinthu zomwe tifuna.

Ngati ife tiononga ndalama kosaganizira kusunga. Sitidzakhala ndi cinthu cabwino. Ndalama ndi cida. Ndi njira yakuguliramo cinthu comwe tifuna, koma osakonda kwambiri ndalama.

YESU NTHAWI ZONSE ALI CIMODZI-MODZI

Nthawi imasintha. Boma limasintha. Anthu amasintha. Yesu sasintha. Lero Yesu ali ndi mphamvu yomwe inamturutsa m'manda. Ndi mphamvu imodzi-modzi yomwe Yesu anali nayo pamene anali pa dziko.

Yesu atilonjeza kutipatsa mphamvu imeneyo ngati timvera ndi kukhulupirira iye. Mphamvu ija, mphamvu ya Yesu Kristu idzatithandiza kukhala ndi cigonjetso mu umoyo wathu.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Kodi muli olimba motani? Kodi mumaimilila pa zikhulupiriro zanu? Kodi mukhulupirira Mulungu zoonadi?

Dziko ndi lodzala ndi anthu ofoka, opanda mphamvu. Palibe yemwe akhoza kusamira pa iwo. Iwo alola dziko kuwapangila cisankho. Ndiye kuti naonso akhala monga anthu osapulumsidwa a m'dziko. Nyumba zao ziri cimodzi-modzi monga za anthu onse. Iwo agwira nchito pa Sabata kuti akhale ndi ndalama zambiri. Iwo sazindikira kuti akonda ndalama. Lankhulidwe lao lifanana ndi ena alionse. Anthu omwe si ali Akristu sawaopa ndipo akhoza kunena cinthu ciri conse pamaso pao. Mpingo wao siukhoza kusamira pa iwo. Abusa ao sakhoza kusamira pa iwo. Mulungu sakhoza kusamira pa iwo, ngakhale kuwagwiritsa nchito.

Mu Cibvumbulutso 3:1-2; Mulungu anauza mpingo wa ku Sardisi zinthu zomwe akhoza kuti uza ife lero: "Ndidziwa nchito zako; muli ndi dina lakuti uli moyo, koma uli wakufa."

Kodi muli akufa? Kodi muli amoyo? Muyenera kusankha ngati muli olola kuimilira Mulungu. Mulungu afunika anthu amene ali ndi zikhulupiriro za mphamvu ndi kuzigwiritsa nchito.

Akristu a cigonjetso akonda abale ao. Yesu anati, 69Kondanani wina ndi mnzace." Akristu acigonjetso athandizana ndi omwe ali osowa.

Mkristu wacigonjetso ndi okhulupirika kwa yemwe anakwatira. Iwo ali ndi nyumba zakukondana, zopemphera, zokhulupirira ndi za cilangizo. Akristu a cigonjetso sazakhumbira zinthu za mwini wace, iwo akhulupirira Yesu, yemwe sasintha. Yesu sadzatilepheretsa ife.

MUTU 9

KWA MPHUNZITSITSI

COONADI: Yesu apatsa cipulumutso kwa onse olandira mphatso yace yaulele.

COLINGA CAKUPHUNZITSITSI: Ndidzagwiritsa nchito phunziro ili kuyesa kutsogolera ophunzira kwa Ambuye ndi ku phunzitsa ophunzira anga momwe akhoza kutsogolera wina ndi mnzace kwa Ambuye.

ZOTHANDIZIRA PAKUPHUNZITSITSI:

Onani kuti mwakonza malo mu cipinda cina kuti anthu awiri akhale patsogolo kucita sowero.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSITSI

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Yesaya 55:1-2 inalembedwa kwa akapolo ku Babulo. Mutu wonse ndi pempho kwa mneneri kuti anthu aturuke mu Babulo ndi kubwelera ku Yerusalemu cifukwa anali atapatsidwa cilolezo.

Poyamba Ayuda analira ndipo anakumbira kubwerera ku dziko lao, Israyeli. Pamene nthawi inapita, anaona kuti kukhala kwao sikunali kobvuta monga momwe anaganizira. Anapatsidwa malo, ndipo anayamba malonda. Iwo anacita bwino pa malonda ao.

Ayuda sanali kudziwikanso kuti anali ansembe ndi aneneri a Mulungu. Anaiwala kuti anali atauza Mulungu kuti adzakhala ansembe a mtundu.

Ndalama, malo ndi nchito zikhoza kuthandiza munthu, koma sizikhoza kutenga malo a kumudzi kumene anacoka. Mulungu anapangitsa mitima ya ana a Israyeli kumva njala ya mau ace. Mtendere unakhoza kupezeka mwa iye yekha.

Mu Yesaya 55:3 tiwerenga kuti Mulungu akali kufuna-funabe otaika. "Tembenukani ndikumvera ine." Mulungu ali kunena. Ngati anthu adzamvera, Mulungu adzakhala ndi moyo. Cikondi ca Mulungu sicingintha. Ngakhale lero Mulungu akali kuitana anthu kuti alape.

Mu Yesaya 55:4-5 ikumbutsa anthu za pangano lomwe anapangana ndi Mulungu. Itikumbusanso za pangano lomwe Mulungu anapanga ndi Davide. Anthu analonjeza kukhala "ansembe a ufumu, mtundu woyera.

Tsopano anali ataiwala mapangano. Anali a malonda, okongolesa ndalama, kulemera ndipo anthu odziwika. Koma Mulungu anapitiriza kuwaitana.

Ngati tifuna kupulumutsidwa, tiyenera kucita zinthu ziwiri. Coyamba, tipemphe Mulungu kutikhululukira macimo athu. Tiyenera kudziwa kuti tinacimwa ndipo tifuna Mulungu kutikhululukira.

Caciwiri, tiyenera kulapa. Tiyenera kusankha kufuna kutikhululukira. Pamene tilapa, titembenuka ku macimo. Titembenukira kwa Mulungu. Ngati tisankha kusatembenuka, ndiye kuti tidzafa mumacimo athu (Luke 13:3).

Yesaya anadziwa kuti cimo iyambira m'mutu. Munthu wocimwa ayenera kusiya maganizao oipa. Ayenera kusintha kacitidwe. Ndipo Mulungu adzamukhululukira. (Yesaya 55:7)

MULUNGU APAMBANA MUNTHU

Mulungu saganiza monga munthu. Sacita monga munthu. Mulungu alibe maganizo oipa monga munthu. Mulungu sacimwa. Ngakhale maganizo ace ndi a akulu kupambana munthu. Mulungu afuna ife kukhala monga iye.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Kodi munalapadi macimo anu? Kodi munaitana Yesu zoonza kukupulumutsani? Kodi munena kuti muli Akristu cifukwa cakuti amai ndi abambo anu ndi Akristu? Kodi musamira pa iwo kukupulumutsani? Simudzapulumutsidwa, pokhapo mutazisankhira nokha.

Ngati ndinu Akristu, kodi cimo ili kukupangitsani kukhala umoyo wogonjetsedwa? Bwanji osalapa macimo anu? Lapani macimo anu kwa Mulungu. Adzakukhululukirani ndi kukuthandizani kukhala monga iye.

Mulungu atikonda ife. Anatikonzequera njira kuti tipulumutsidwe. Tiyenera kulapa macimo athu ndi kukhulupirira mwa Mwana wa Mulungu. Mulungu adzatikhululukira timlemekeza iye.

MUTU 5

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Yesu adzathandiza Akristu kukhala ndi umoyo wa cigonjetso.

COLINGA CAKUPHUNZITSA: Phunziro ili idzapatsa ophunzira anga ndi ine danga lakudziwa kapena ngati tiri otsutsidwa ndi kuti tiri kukhala umoyo wa Mulungu.

ZOTHANDIZIRA PA KUPHUNZITSA: Palibe.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA:

Mu Ahebri 13:1-3, mlembi acenjeza ife kuti tikonde abale athu. Pamene cikondi ca kwa abale athu cicepa, cikondi ca Mulungu naconso cicepa. Owerenga alikulimbikistidwa mu kalata iyi kulandila alendo, kudya ndi kuceza nao mu nyumba zathu.

Anakumbutsa anthu kuti kuitana anthu mu nyumba zathu tikhoza kukhala ndi danga la kucezera angelo monga Abrahamu anacita. Akristu oyamba analonjeza kucezerana ndipo iwo anacita ici.

Analimbikitsa owerenga kucezera omwe ali mndende. Ambiri anali mndende pa nthawi imeneyo. Odwala anafunika kusamalilidwa cifukwa anali mbali ya thupi la Kristu.

Ahebri 13:4 itipatsa malangizo a cikwati coyera. Pa nthawi imeneyo anthu ambiri sanali kukwatirana. Iwo anazipereka kucitira umboni ndi kuphunzitsa Akristu atsopano. Nthawi zambiri anali kukhala pamodzi, koma sanali kukhala thupi limodzi. Kuyera kwao kunadabwitsa Aroma omwe anali kukhala nao. Iwo anadabwa cifukwa Akristu anakhoza kukhala osacita cigololo.

Koma ngakhale tero, kapena panali bvuto pakati pao. Kapena iwo anayamba kuganiza kuti umoyo wao woyera unapambana Akristu ena omwe anali okwatira. Kuzikonda kunalowa mu mitima mwao. Mlembi apa alikuwauza kuti asanene zoipa kwa anthu omwe ali mu cikwati.

Anthu omwe ali okwatira anayenera kusunga cikwati kukhala coyera. Iwo anafunika kukhala okhulupirika kwa wina ndi mnzace.

Ndime 5 itiuza kuti tisakonde kwambiri ndalama. Ndime iyi, ndi ija ya cigololo ziyendera pamodzi, cifukwa nthawi zambiri macimo awiri awa amayendera

pamodzi. Tiyenera kukhutira ndi zomwe tiri nazo, cifukwa Mulungu aona kuti tisasowe kanthu.

Ndime ya 6 inena mau a ku Salmo 118:6. Ici cilimbitsa Akristu kugwirira ku zikhulupiriro zomwe ali nazo mwa Mulungu. Mulungu apambana munthu.

Ndime ya 7 itiuza kukumbukira omwe anayenda patsogolo pathu, omwe anali okhulupirika kufalitsa uthenga kwa ife. Tiyenera kuyelekeza cikhulupiriro cao.

Ndime ya 8 itipatsa cikondwerero. Yesu sasintha. Iye ndi yemwe tiyenera kuyelekeza. Iye ali cimodzi-modzi.

Ndime ya 20-21 ndi pemphero kwa owerenga. Wolembe anapempha kutipempherera mu ndime zimenezi.

Anapempha Mulungu kupatsa Akristu zinthu zofunikira kuti iwo akwaniritse kucita nchito yomwe anawakonzekera. Uyu ndi Mulungu wa mtendere anaukitsa Yesu. Yesu ndi mbusa wa nkhosa. Iye anapereka mwazi wace kukwaniritsa pangano.

Atsiriza kalata wace pa kupatsa yesu ulemmero wa muyaya.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO ILI

Kudziwitsa

Nenani: “Panali munthu wina wachedwa Yohane. Yohane ananena kuti anali Mkristu. Anali kupita kumpingo sabata ndi sabata. Anali wophunzira mu gulu la maphunziro a Mbuku Lopatulika. Nthawi zambiri anali kupereka umboni kumpingo. Anati ali Mkristu. Abusa anakumbukira pamene anabatizidwa.

Pakati pa sabata, Yohane anali kucita zinthu zomwe anthu onse anali kucita. Anali kucezera mai wina kawiri pa sabata nthawi ya usiku. Iye anafuna kuti mkazi wace aganize kuti ali ku nchito. Ici ndi comwe anamuuza. Iye sanali kukoka fodya, koma anali kukoka ngati wina ampatsa. Anakonda kumva zomwe zinali kucitika mu mzindamo.

Nthawi zambiri Yohane anali kukhala umoyo monga wakunja. Kodi mudziwa munthu wina ali monga Yohane?

KUMASULIRA

Nenani: “Mlembi wa Ahebri sanafune owerenga ace kukhala monga Yohane. Iye anafuna iwo kukhala ndi umoyo wa cigonjetso. Mu phunziro la lero, awapatsanso malangizo ena.”

Kodi munakhalapo ndi ludzu? Ludzu ndithu? Munafuna-funa cakumwa. Anthu akhoza kukhala opanda cakudya kwa kanthawi, koma sakhoza kukhala kopanda kumwa madzi. Mathupi athu afunika madzi.

Mathupi athu auzimu naonso afuna kudya. Anthu ena amafunitsitsa cakudya ca kuuzimu. Yesaya anadziwa kuti mizimu yathu inafunika cakudya ndi madzi a kuuzimu. Yesaya anati, “Bwerani kwa Mulungu.”

Ana a Israyeli, omwe anali anthu a Mulungu osankhidwa, anakana kumvera Mulungu. Anali kukhala umoyo wocimwa. Yesaya anawauza kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi. Mpulumutsi anali kubwera kupulumutsa anthu onse omwe anakhulupirira mwa Iye. Aliyense anaitaidwa kudza. Anthu omwe analibe ndalama anaitanidwa kudza.

Aliyense akanakhoza kudza kwa Mulungu. Cisomo ca Mulungu cikanapita kwa aliyense amene anabwera kwa iye. Cisomo cace cikanapanga anthu kukhala okondwa. Anthu ayesa kugula zinthu kuti ziwakondweretse, koma sakhoza kukondwa. Munthu anagwira nchito molimba, koma sanakhoze kukhala wokondwa. Mulungu yekha ndiye akhoza kukwaniritsa zosowa za munthu, za kuthupi ndi za kuuzimu.

PANGANO LA MULUNGU LOSATHA

Mulungu anali ndi uthenga kwa anthu ace. Anafuna kuti iwo amumvere. Anafuna kuti acite zomwe iye anafuna.

Mulungu anapanga pangano ndi mfumu Davide. Werengani 2 Samuuli 7:8-16. Mulungu analonjeza kukonda anthu a Israyeli. Anawalonjezanso kuwalanga ngati anacimwa, ngati iwo sanamvere Mulungu. Mulungu anafuna Israyeli kukonda ndi kumvera iye.

Davide anali Mfumu ya Israyeli. Anali mtsogoleri wao. Yesaya anauza anthu a Israyeli kuti Mulungu adzatumiza wina owatsogolera. Iye adzakhala Mpulumutsi Wozunzika (Yesaya 53). Iye adzalipila mtengo wa macimo a anthu. Yesu Kristu anali Mpulumutsi wozunzika. Analipila mtengo wa macimo a anthu ambiri omwe anakhulupirira mwa iye. Pangano la Mulungu latsopano, pangano losatha, inakwanilitsidwa ndi Yesu Kristu.

MULUNGU AKHULULUKIRA CIMO

Werengani Yesaya 55:6-7 kaciwiri. Mulungu afuna kutikhululukira macimo athu, koma tiyenera kufuna kukhululukidwa. Mulungu nthawi zonse sadzakhala pafupi. Sitikhoza kutsimikiza kuti tidzakhala ndi moyo mawa. Lero tikhoza kudziwa kuti tiri amoyo. Lero tikhoza kudziwa kuti tikhulupirira mwa Iye. Lero tikhoza kudziwa kuti tidzapulumutsidwa.

MUTU 9

CIKONDI CA MULUNGU

COLINGA: Phunziro ili idza ndiphunzitsa kulapa ndi kutembenukira kwa Mulungu. Kapena momwe ndingatsogolere wina kwa kucita ici.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Salmo 136; Yesaya 55; 2 Samueli 7:8-16.

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Yesaya 55:1-9, 2 Samueli 7:8-16

MAU APAMTIMA: *“Yamikani Yehova pakuti ndiye wabwino: Pakuti cifundo cace ncosath.”* (Salmo 136:1)

Pa nthawi ya kukonzekera citsitsimutso, Akristu atatu anali kupita ku nyumba ili yonse mu dela limenelo. Anagogoda pa khomo lina. Bambo wina anaturuka m'nyumba muja. Kaonekedwe kace kanacititsa mantha azimai aja, koma wina analimba mtima.

“Bambo” anatero, “Yesu akukondani ndipo afuna inu kukhulupirira mwa Iye.” Ndi misozi m'maso ace munthu uja anati, “Palibe yemwe akonda ine.”

Moleza mtima azimai a Cikristu ananena za Yesu ndi momwe anakondera bambo uja.

Aliyense afunika kudziwa kuti Mulungu amukonda. Afunika kudziwa kuti wina asalimalira iwo.

Ana a Israyeli nthawi zambiri sanamvere Mulungu. Iwo sanabwezere cikondi ca Mulungu. Iwo sanakhulupirire mwa Mulungu. Iye anapitiliza kusunga iwo. Ndiponso anapitiliza kusunga mbali yace ya pangano yomwe anapanga ndi iwo.

Mulungu sasintha maganizo ace, ngakhale kuswa Mau ace. Cikondi cace ncamuyaya. Tikhoza kumukhulupirira kuti adzatikonda nthawi zonse.

KUITANIDWA KWA ANTHU ONSE

Werengani Yesaya 55:1-9. Pamene wina akuitanani kunyumba yao kuti mukadye nao, muyenera kunena iai kapena inde. Sadzakukamizani kupita kunyumba yace. Cisankho ciri kwa inu.

Mulungu aitana anthu onse kubwera kwa iye. Mulungu alimbikitsa anthu onse kubwera kwa iye. Koma Mulungu sadzakakamiza aliyense kubwera kwa iye. Iwo ayenera kubwera cifukwa afuna kubwera.

Uzani ophunzira anu kutsegula mabuku Opatulika ao ku Ahebri 13. Wina pa 1 Akorinto 15:58, wina awerenge 1 Akorinto.

Nenani: “Paulo anena kuti tiyenera kukhala osagwedezeke. Kodi Paulo atanthauza ciani?” Apatseni nthawi kuti alakhuzane. Atsogolereni kuti adziwe kuti cikhulupiriro cao ciyenera kukhala colimba mwa Mulungu. Tiyenera kukhala okonzekera kuimirira Yesu. Tiyenera kukhala ndi umoyo omwe anthu adzaona kuti ndife Akristu.

Funsani: “Kodi ndi langizo lotani lomwe mlembi ali kutiuzi? Aloleni alankhuzane. Onjezani ngati ziripo. Pitirizani kufunsa ngati langizo ikali labwino kwa ife lero?”

Pamene muganiza kuti ophunzira anu amvetsetsa tanthauzo la ndime izi, awerengeleni ndime labwino la 20-21.

Nenani: “Iyi ndiyo nthawi yokha yomwe mlembi wa Ahebri agwiritsa cithunzi-thunzi ca Yesu monga mbusa. Iye atisamalira bwino monga momwe mbusa asalimalira kamwana kanyama. Mulungu nthawi zonse amatipatsa zofunikira kuti ticite nchito yace yomwe afuna kuti ticite. Atipempha ife tonse kukhala umoyo wa cigonjetso ca Cikristu. Tiyenera kumukhulupirira ndi kumvera.”

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Pemphani wophunzira wina kuwerenga mbali yochedwa “Comwe citanthauza kwa ine” Kucokera ku mabuku ao.

Nenani: Padziko lapansi anthu ambiri ali kubadwa kwambiri kupambana omwe ali kupulumutsidwa. Colepheretsa ndi cakuti Akristu siali kukhala umoyo wolimba. Ali kulephera kugawa uthenga kwa anthu owazungulira. Iwo akhoza kukhala nazo zikhulupiriro, koma osazonetsera mu umoyo wao. Akhoza kudana ndi cimo koma ali ofoka ndipo saleka kucimwa. Mulungu aitana Akristu lero kukhala umoyo wa Cikristu wa cigonjetso. Atitana kutaya “Cimo yomwe igwiririra. Kodi tiri okonzeka kuyankha maitanidwe ace? Pemphani ophunzira anu kugwetsa nkhope zao. Yambani pemphero pa kulapa kwa Mulungu zomwe mwalephera. Ndipo funsani wophunzira wina kulapa monga momwe inu mwacitira. Pitirizani kufikila onse atakhala ndi nthawi ya kupemphera. Ndipo tsekani ndi pemphero pa kupempha Mulungu kuti mukhale umoyo wa cigonjetso.

MUTU 6

ULEMERERO WA MULUNGU MU CILENGEDWE

COLINGA: Phunziro ili idzandithandiza kukhulupirira Mulungu mokwanira mu mabvuto anga.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Salmo 104

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Salmo 104:24-34

MAU APAMTIMA: *"Nchito zanu zicurukadi, Yehova! Munazicita zonse mwanzero; Dziko lapansi lidzala naco cuma canu."* (Salmo 104:24)

Sabata lino tiyamba ziphunzitso zofunikira za m'Cipangano Cakale. Ziphunzitso izi zidzatithandiza kukomana ndi mabvuto mwa cikhulupiriro. Zionetsa kasamalidwe ka Mulungu. Pamene tidziwa kuti atisamalira, tikhoza kumukonda ndi kumukhulupirira.

Mlembi wa Salmo 104 anayamika Mulungu pamene anaona zinthu zomzungulira zomwe Mulungu analenga. Cinthu ciri conse ciri ndi colinga. Mlembi anazindikira kuti mphamvu ya Mulungu inalenga zonse, isunga dziko dziko kupitabe patsogolo.

Mphamvu ya Mulungu ikali kusunga dziko, mlenga-mlenga, kupitabe patsogolo bwino. Mphamvu yace ikali kulenga zinthu zabwino. Akali kupatsa munthu zonse zimene afuna kuti akondwere. Tiyenera kuyamika Mulungu cifukwa ca cilengedwe cace.

MULUNGU ANALENGA ZINTHU ZONSE

Mu Salmo 104, woyimba ali kuyamikira Mulungu cifukwa ca cilengedwe cace. Anadziwa kuti Mulungu anali wamphamvu ndipo wanzero cifukwa anapanga dziko lonse. Anayang'ana pa nyanja ndi zomwe zikhala momwemo. Nyama za m'nyanja zinali zambiri kuti ziwerengedwe.

Mulungu analenga cinsomba cikulu ndipo alamulira pa ico. (Werengani ndime 26 kaciwiri) Mmamasulidwe ena a Buku Lopatulika anena kuti anacipanga kukondwera naco. Cimakondweretsa Mulungu kuona zilengedwe zace ziri zokondwa.

MULUNGU ASAMALIRA ZILENGEDWE ZACE ZONSE

Werengani Salmo 104:27-30. Zilengedwe za Mulungu zisamira pa iye. Mulungu amapatsa cakudya, malo ogonapo a nyama ndi mbalame. Azipatsa umphweya, cakudya ndi madzi akumwa.

ca moto. Kuitanidwa uku kunapangitsa Mose kupita ku Aigupto kuturusa anthu. Eksodo 3:12 itiuza zomwe Mulungu anamuza. "... Ine ndidzakhala ndi iwe; ndipo ici ndi cizindikilo ca kuti ndakutuma ine; utaturusa anthuwo mu Aigupto, mudzatumikira Mulungu pa phiri pano." Conco Mulungu anakwaniritsa lonjezo lace kwa Mose pamene anatsogolera anthu ku phiri la Sinai. Inali nthawi ya Mose kutumikira Mulungu pa phiri, iye anafunika kukhala pakati pa Mulungu ndi anthu pa kupanga pangano.

"Pangano inali yaitali ndipo yofotokezedwa bwino. Mbali yaikulu inali malamulo khumi. Izi zinalembedwa pa magome a miyala. Tidzaphunzira malamulo amenewa lero."

Kugwiritsa nchito buku la Eksodo 20:1-17, lolani ophunzira alankhuzane pa malamulo onse. Ici cidzatenga nthawi. Ngati pali nthawi, funsani ophunzira anu kuti "Ufumu wa ansembe utanthauza ciani?"

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Nenani: "Malamulo khumi apanga madziko a mitundu yambiri. Ngati timvera malamulo khumi amenewa, tidzakhala mu mtendere ndi mciyanjano ndi Mulungu pamodzi ndi munthu. Munthu akhoza kuyesa kusunga malamulo onse koma kukhalabe wotayika. Kumvera malamulo khumi sikubweretsa cipulumutso. Yesu ndiye njira yokha ya cipulumutso."

Nenani: "Ndi cabwino kusunga malamulo, ndipo tiyenera kuyesa kutero. Koma tiyenera kukumbukira kuti Yesu ndi pangano latsopano monga momwe tinaphunzirira mu phunziro lacinatu. Yesu atiuza kuti ndiye njira kuti tikhale mciyanjano ndi Mulungu. "Ngati muli pano lero ndipo mufuna kupulumutsidwa, salirani pang'ono kuti tilankhuzane momwe mungapulumutsidwire."

Nenani: "Sabata latha, tinalankhula za kuyamika Mulungu. Kodi ndi angati a inu sabata lino omwe anapeza nthawi ya kuyamikira Mulungu? Lolani ophunzira anene za kukwaniritsa kwao kapena kulephera kwao kuyamika Mulungu. Ndipo tsekani ndi pemphero ya ciyamiko monga momwe munacitira sabata latha.

Ana a Israyeli anafunika kuphunzitsidwa, pa kuwabvumbulutsira, za khalidwe ndi kupembedza Mulungu woona. Anafunika kuphunzitsa mitundu yonse za Mulungu. Ici cinaonetsa kuti Mulungu anali akali kukonda dziko, osati ana a Israyeli okha. Iwo anafunika kuonetsa dziko cikondi cimeneci.

Mu Eksodo 20:1-17 Mulungu anapatsa anthu malamulo khumi atabvomereza pangano. "...Zonse zimene Mulungu anena tidzacita." (Eksodo 19:8) Mulungu analemba malamulo pa mwala ndi kuwapereka kwa Mose (Eksodo 32, 15-16)

Malamulo khumi apatsa Mulungu danga la kuuza anthu zinthu zitatu za iye. Coyamba, zitiuza kuti Mulungu ndi yani. Iye alipo. Sanangolenga munthu ndi kupita ku dziko lina. Iye akhala pano ndipo afuna kudziwa za umoyo wathu, za munthu ndi cilengedwe cace.

Cinthu caciwiri, malamulo khumi atiuza kuti Mulungu alankhula kwa anthu. Mose anamva mau ace ndi kuwauza kwa ana a Israyeli. Cinthu ca citatu comwe lamulo itiuza ndi cakuti Mulungu atsogolera anthu mu umoyo wao wa masiku onse.

Malamulo khumi onse sali pangano. Anaikidwa mu madela. Mwacitsanzo, munthu aletsedwa kupha koma malamulo khumi satiuza zinthu zina zomwe sanafunike kucita. Tidziwa kuti nyama zina zinali kuphedwa mukacisi za nsembe. Malamulo khumi analetsa kupembedza milungu ina, koma analephera kumasulira kuti kupembedza kweni-kweni nciani. Malamulo khumi anali nchito yomwe inali kuonetsa za mtsogolo.

Kumasulira kwa malamulo onse awa kupatsidwa mu buku la ophunzira.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

KUDZIWITSA

Nenani: "Pamene mwamuna ndi mkazi alonjezana kukondana, ndi kulemekeza wina ndi mnzace umoyo wao wonse, iwo apanga pangano. Yense wabvomekeza kukhala okhulupirika kwa wina ndi mnzace. Ndi pangano yomwe ikhala kufikira wina atafa.

"Phunziro lathu lero linena pa pangano pakati pa Mulungu ndi munthu."

KUMASULIRA

Uzani ophunzira kutsegula ku Eksodo 19:3-6. Werengani ndime izi kwa ophunzira.

Nenani: "Ana a Israyeli anali atayenda kwa miyezi itatu asanifike pa phiri la Sinai. Ici ndico cinali colinga cao pamene anacoka ku Aigupto cifukwa apa ndipo pa phiri pomwe Mulungu analankhula ndi Mose kupyolera mucisamba

Mulungu analenga munthu ndi nzeru kuti aganizire, maso kuto aone, makhutu kuti amve, manja kuti agwire nchito. Mulungu anapatsa Munthu thupi la nthanzi ndi mphamvu kuti agwire nchito. Mulungu amampatsa munthu zofunikira zonse.

Ngati Mulungu sakanasamalira zilengedwe zace zikanafa. Mulungu anapanga nsomba kuti zidzikhala m'madzi. Nsomba yomwe icotsedwa m'madzi imafa mwamsanga.

Mulungu apatsa moyo ndipo amalandanso. Mulungu apatsa cakudya ndi thupi la nthanzi kwa zilengedwe zace zonse. (Ndime 30)

YAMIKANI MULUNGU PA CILENGEDWE CACE

Mlembi apitiridza kuyamikira Mulungu mu ndime 31 ndi 34. Pamene anapitiridza kuona cilengedwe ca Mulungu, anayamba kupembedza ndi kuyamikira Mulungu.

Mulungu anayang'ana pa cilengedwe cace. 169Ndipo Mulungu anazona zonse zimene iye anapanga, ndipo zinali zabwino..." (Genesis 1:31).

Mlembi anafuna kuyamika Mulungu. Anayamika Mulungu kupyolera mu nyimbo ndi mapembedzo. Anaganizira za Mulungu. Anaganizira momwe anakondera Mulungu ndi cilengedwe cace.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Ngati Mulungu asalalira nyama, mbalame ndi maluwa, ndiye kuti akhoza kutisamalira ife. Munthu ali cilengedwe copambana ca Mulungu. Munthu analengedwa mu cifaniziro ca Mulungu. Anamuika iye kulamulira pa zilengedwe zonse. Mulungu akonda ndipo asalalira munthu. Mulungu afuna kuti munthu amkonde ndi kumpembedza Iye. Kodi mukonda Mulungu motani?

Akhoza kuyamika Mulungu pa dziko lace la bwino. Tikhoza kumuyamika pa cikondi cace, ndi kutipatsa zofunikira masiku onse. Tikhoza kuyimba nyimbo kwa Mulungu ndi kumupembedza.

Musanagone lero, yamikani Mulungu pa cakudya comwe mwadya. Muyamikeni pa cifukwa ca nthanzi lanu. Muyamikeni cifukwa ca ana anu, abusa ndi mpingo wanu. Muyamikeni pa madalitso omwe akupatsani masiku onse.

Sabata lino yesani kupemphera pemphero imodzi ya ciyamiko kwa Mulungu. Mu pemphero, yamikani Mulungu cabe. Yesani kuganizira zinthu zomwe akucitirani. Musapemphe cinthu ciri conse mu pemphero iyi. Yamikani cabe.

Kapena nthawi yoyamba pamene mudzacita izi, pemphero lanu lidzakhala lalifupi.

Pamene mupitiliza kuganizira zinthu zomwe mukhoza kuyamikira Mulungu, ikani m'mundandanda zinthu izi. Pamene mundandanda ukula mudzakhala okondwa ndi ciyamiko. Kumuyamikira Mulungu ndi njira ina yakunena kuti mumukonda.

Mulungu anagwiritsa nchito nzeru zace ndi mphamvu kulenga zinthu zonse. Anaona kuti zonse zomwe analenga ndi zabwino. Mulungu asalimalira zilengedwe zace zonse.

Mulungu apatsa cilengedwe cace copambana (munthu) zofunikira. Mulungu amatisamalira.

Tiyenera kuyamika Mulungu, kukonda Mulungu ndi kumupembedza pa zinthu zonse zomwe anaticitira.

MUTU 8

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Akristu ayenera kumvera Mulungu kuti asunge pangano ndi ine.

COLINGA CAKUPHUNZITSA

Ndifuna ophunzira anga kuti ayenera kukhala ndi umoyo wonva Mulungu ngati afuna kukhala mu mtendere ndi iye. Ndifuna ophunzira anga omwe asanakhale Akristu kudziwa kuti akhoza kulowa mu pangano ndi Mulungu.

ZOTHANDIZIRA PAKUPHUNZITSA Palibe.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Werengani Eksodo 19:3-6. Mose anali atatsogolera ana a Israyeli kucokera ku Aigupto kupita kucipululu. Mulungu anali atawalonjeza dziko la Kanani.

Pamene asanalowe mu dziko la Kanani, anafunika kuumbidwa monga mtundu. Tsopano Mulungu anali okonzekera kuwapanga kuti akhale mtundu, anafunika kukhala ogwirizana. Anafunika kupembedza Yehova Mulungu, Mulungu woona wamoyo.

Mulungu anadziwa kuti monga mtundu, anafunika malamulo owatsogolera. Mulungu anaganiza kupanga pangano ndi iwo.

Mu pangano liri lonse kumafunika zinthu zomwe mumagwirizana. Nthawi iyi ana a Israyeli pamodzi ndi Mulungu anabvomekezana. Mu Eksodo 19:5, Mulungu anaika zinthu zomwe anabvomekezana.

a) Ngati mumvera liu langa ndi

b) Kusunga pangano langa, ndipo

c) Mudzakhala zida zanga pakati pa anthu

d) Ndipo mudzakhala ufumu wa ansembe, ndipo

e) Mudzakhala mtundu woyera.

Kumvera Mulungu inali mbali ya pangano madalitso apadera, kucinjiriza, cuma ndi mtundu zinaikidwa padera kusunga nzeru ndi kupembedza Mulungu inali mphatso yao.

kukhumbira cinthu ca mwini.

Malamulo khumi awa anapatsidwa kwa anthu kuwathandiza kukhala mu mtendere kwa wina ndi mnzace.

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Masiku ano anthu amanama bodza, kuba ndi kucita zinthu zina kuti atenge zomwe afuna. Ngati ife ndi ana a Mulungu oona, sitidzakhala monga tere.

Kodi muli kumvera Mulungu? Kodi muli kusunga malamulo ace? Pamene munthu asunga lamulo, apanga Kristu kukhala Mbuye wa moyo wace. Kodi Kristu ndi Mbuye wa moyo wanu?

MUTU 6

KWA MPHUNZITSI

COONADI: Mulungu atisamalira kupambana cinthu cina ciri conse.

COLINGA CA KUPHUNZITSA; Ndifuna ophunzira anga kuyamba ku lemekeza Mulungu mu umoyo wao. Kupyolera mwa ici ndifuna kuti azindikire kuti Mulungu awasamalira kopambana cinthu cina ciri conse.

ZOTHANDIZIRA PAKUPHUNZITSA

Pepala ndi colembela kwa wophunzira aliyense.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUDZIWITSA

Salmo 104:24-34 ndi ndime zomwe tidzaphunzira mu phunziro ili. Wolemba Masalmo anali wokondwera kwambiri ndi cilengedwe ca Mulungu. Iye anali atangochula maina a zinthu zomwe Mulungu analenga. Ndipo ananena kuti, nchito ya Mulungu ya cilengedwe ndi yambiri. Anayamikira Mulungu cifukwa ca nzeru zace. Cifukwa Mulungu analenga zinthu zambiri.

Ndime ya 25 itiuza za nyanja ndi kakulidwe kace. Imasunga nyama zazikulu ndi zazing'ono. Pali nyama yaikulu yomwe wolemba Masalmo sakhoza kuganizira kukula kwace. Koma ngakhale ndi yailulu ikhoza kukhala mu nyaja. Ngalawanso zimayenda pa nyanja.

Ndime 31 iyamikira Mulungu ndi kulemekeza iye. Wolemba Masalmo anena kwa Mulungu kupedza cikondwerero mu zinthu zomwe analenga.

Ndime 32 itionetsa mphamvu ya Mulungu yomwe ikhoza kukuza maphiri ndi kuwapangitsa kunjenjemera. Ngakhale dziko limanjenjemera Mulungu atali khuza.

Ndime 33 ndi 34 ionetsa kuti wolemba Masalmo anadabwitsidwa ndi zinthu zomwe anaona. Analonjeza Mulungu kuti adzamyimbira mu umoyo wace wonse. Anapempha Mulungu kuyang'anitsa pa kuzipereka kwace ndi cikondwerero. Iye anakondwera mwa Ambuye, ndipo anaitana Mulungu kukondwera mwa iye.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO ILI

Kudziwitsa

Nenani: “Lero tidzayamba maphunziro a mu Cipangano Cakale. Maphunziro awa adzatithandiza kudziwa kuti Mulungu atikonda ife. Adziwa zonse zomwe zicitika kwa ife. Adziwa pamene tiri ndi mabvuto, adziwa pamene tiri mu cikondwerero. Iye amakonda kumvera pamene tilankhula kwa iye. Amakondwera kumvera ciyamiko pa nchito yomwe anacita.

“Kuyamba phunziro lathu lero, ndifuna kuti tipange mndandanda wa mayamiko ndi mau ena ocokera mu Masalmo. Anthu ambiri sadziwa kupemphera mapemphero a ciyamiko. Kulankhula kwao ndi Mulungu ndi kupempha. Iwo sanapempherepo pemphero la ciyamiko ndi ya kutamanda. Pena cowalepheletsa ndi kusadziwa kuyamika Mulungu. Iwo sadziwa mau omwe akhoza kugwiritsa nchito pa kuyamika Mulungu. Tidzaona mu Masalmo ndi kupeza mau omwe tikhoza kugwiritsa nchito pa kuyamikira Mulungu.”

Tengani nthawi yaikulu kucita cinthu ici. Ngati palibe cina cimene mwaphunzitsa, cidzakhala cabwino iwo kudziwa kuyamika Mulungu.

Pena mudzafuna kulemba mudandanda pa bolodi kapena wophunzira wina alemba. Onani kuti wophunzira aliyense atenga mndandanda umodzi, kunyumba.

Mundandanda udzakhala ndi izi zonse. Ndicofunikira kwambiri kuti ophunzira anu apeze mau awa mu Buku Lopatulika pa iwo okha. Pamene iwo apedza imodzi akhoza kunena pomwe iwo aipedza, kuti ena awerenga naonso.

1. “Ndidzakukwezani, Yehova....” (Salmo 30:1)
2. “...ndidzakuyamikani nthawi zonse.” (Salmo 30:12)
3. “Ndidzakondwera ndi kusangalala....” (Salmo 3:7)
4. “Sekerani mwa Yehova...” (Salmo 32:11)
5. “Yimbirani zoyamika Yehova...” (Salmo 9:11)
6. “Ndidzayamika Yehova ndi mtima wanga wonse (Salmo 9:1)
7. “....Ndidzagwada ...” (Salmo 5:7)
8. “...Nasekera mwa inu iwo akukonda dzina lanu” (Salmo 5:11)
9. “Nkokoma kuyamika Yehova ...” (Salmo 92:1)

NCHITO YA MUNTHU KWA MULUNGU

Lamulo loyamba (Eksodo 20:3) inanena kuti sanafunike kupembedza Mulungu wina. Iye ndiye yekha Mulungu wona. Anafunika kukhala woyamba mu umoyo wao.

Lamulo laciwiri (20:4) inena kuti analetsedwa kupanga mafano kuti apembedze. Anthu ena akanapembedza mafano koma osati ana a Israyeli.

Lamulo la citatu (20:7) inawauza kuti asachule dzina la Mulungu pacabe. Anthu anafunika kugwiritsa nchito dzina limenelo ndi ulemu.

Lamulo la cinai (20:8) inaike tsiku la kupembedza. Mulungu tsiku ili anapuma. Pamene atsiliza kulenga zinthu zonse mu masiku asanu ndi imodzi, tsiku lotsatira anapuma. Werengani Genesis 2:3. Tsiku ili linayamba kuchedwa Sabata mu Eksodo 16:23. Ndipo inafunika kukhala tsiku la kupumula.

Yesu anauka kwa akufa pa tsiku loyamba la Sabata. Cifukwa cace, lero Akristu ambiri ali kupembedza pa tsiku loyamba la Sabata, Sabata, pa kukumbukira zomwe Yesu anacita kwa iwo.

Malamulo onse anai inali nchito ya munthu kwa Mulungu. Koma munthu anali ndi nchitonso ina. Izi zinali kwa anthu ena.

NCHITO YA MUNTHU KWA ENA

Lamulo la cisanu (20:12) iwauza kulemekeza atate wao ndi amao. Mulungu apatsa moyo kupyolera mwa makolo. Tiyenera kuwapatsa ulemu. Pamene tilephera kuwapatsa ulemu, tipwanya lamulo la Mulungu.

Lamulo la cisanu ndi cimodzi (20:13) iletsa kupha. Mulungu yekha ndiye apatsa moyo. Ndiponso Mulungu yekha ndiye akhoza kutenga moyo wa munthu.

Lamulo la cisanu ndi ciwiri (20:14) iwaletsa kucita cigololo. Mukacita ici kopanda cikwati mupwanya lamulo la Mulungu.

Anthu ena anena kuti nthawi yasintha ndiponso akhoza kuiwalako za lamulo ili. Koma lamulo la Mulungu silisinthika. Mau ace ali cimodzi-modzi masiku onse. Lamulo la cisanu ndi citatu (20:15) iloza kwa anthu ambiri masiku ano. ikuti, “Usabe.” Palibe yemwe aloledwa kutenga cinthu camwini.

Lamulo la 9 (20:16) itiuza kuti tisanene bodza. Nthawi zonse tiyenera kunena coonadi. Sitiyenera kunena zinthu zonama kwa ena.

Lamulo la 10 (20:17) itiuza kuti tisasilire. Kusilira citathauza kufuna cinthu cimeneco kwambiri kuti sitiganiza cinthu cina. Tiuzidwa makamaka kusiya

MUTU 8

PANGANO LA MULUNGU NDI MUNTHU

COLINGA: Ndidzaphunzira kuti ndinasankhidwa ndi Mulungu kukhala oyera, ndipo wokhulupirika kwa iye.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Eksodo 19, 20, 32, 34.

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Eksodo 19:3-6, 20:1-17

MAU APAMTIMA: *“Ndipo anatenga buku la Cipangano, nawerenga m’makutu a anthu, nati, taonani mwazi wa cipangano, cimene Yehova anacita nanu, kunena za mau awa onse,”* (Eksodo 24:7).

Pangano linapangidwa pakati pa anthu ndi Mulungu. “Pangano” litanthauza cibvomekezo pakati pa anthu awiri kapena ambiri. Pangano lomwe Mulungu anapanga linali pakati pa Iye ndi Israyeli. Mulungu analonjeza kuwasamalira iwo. Analonjeza kumvera Iye. Tsegulani ku Mutu wa 3 mu buku ili ndi kuphunziranso ziphunzitso za pangano pakati pa Mulungu ndi anthu.

MULUNGU ANALANKHULA KWA MOSE

Werengani Eksodo 19:3-6 ndi Eksodo 20:1-17. Mose anali atagonjetsa Farao kulola ana a Israyeli kubwelera ku Kanani. Mose anawatsogolera kuturuka mu Aigupto kupita mu cipululu.

Pamene anafika ku Phiri la Sinai, Mose anapita pamwamba pa phiri kulankhula ndi Mulungu. Mulungu anapatsa Mose uthenga kupereka kwa ana a Israyeli.

Mulungu anakumbutsa anthu pamodzi ndi Mose momwe anawasamalira iwo. Pamene anali akapolo, anapemphera kuti amasulidwe. Mulungu anayankha pemphero lao. Analonjeza kuwasamalira iwo. Anasunga lonjezo lace pamene anawaturutsa mu Aigupto.

Mulungu anawauza za lonjezo lomwe akanapangana nao. Werengani Eksodo 19:5-6 kaciwiri. Ana a Israyeli anafunika kupatsidwa ulemu kwambiri. Mulungu akanawasankha kukhala anthu ace ngati iwo akanakhala omvera Iye. “Akanakhala ansembe a ufumu.” Nchito yao inali ya kuuza anthu za Mulungu.

Pangano linafunika kupangidwa ndi anthu onse. Siinali la ana a Israyeli okha. Onse anafunika kubvomera. Conco Mulungu anapanganso pangano ndi mtundu wonse. Mbali yofunikira kwambiri ya pangano inali la malamulo khumi.

10. Ndi kuyimbira nyimbo dzina lanu... (Salmo 92:1b)

11. “...Kuonetsera cifundo canu mamawa ...” (Salmo 92:2)

12. “ndidzapfuula mokondwera....” (Salmo 92:4)

13. “Yamikani Yehova...” (Salmo 105:1)

14. “Mudzitamandire ndi dzina lace loyera” (Salmo 105:3)

15. Ndimkonda Mbuye, popeza Yehova amamva... (Salmo 116:1)

Tthandizani ophunzira anu kuona kuti akhoza kugwiritsa nchito mau awa pa kuyamikira Mulungu. Pemphero ikhoza kukhala motere “Adalitsike Mulungu, ndi kukondani cifukwa munandikonda poyamba. Ndimayimba ndi cimwemwe pamene ndiganizira kuti munandikonda ngakhale ndisanabadwe. Ndiyamikira inu, Mbuye wanga, cifukwa mwandisunga bwino kucoka ku zoipa. Ndinena za cikondi canga kwa inu m’mamawa pamene ndiuka. Ndikulemekezani cifukwa munalenga dziko labwino lomwe ndikhalamo. Ndi kukukuzani cifukwa mudziwa kunena nthawi zonse.”

Pamene ophunzira anu adzadziwa kumvetsetsa mau omwe akhoza kugwiritsa nchito pa kuyamikira Mulungu, adzayamba kuyesa kuyamikira. Auzeni kuti asunge mndandanda wao mu Mabuku Opatulika ao. Kutu iwo pamene apemphera akhoza nchito mundandanda umenewu kulemekeza Mulungu kufikira atakhoza kucita tero kopanda kugwiritsa mndandanda.

Nenani: “Mulungu yemwe tipembedza ndi Mulungu wabwino. Phunziro lathu ndi la cilengedwe ca dziko.”

KUMASULIRA

Ophunzira anu atsegule mabuku ao ku Salmo 104:24-34, ndipo awerenge.

Funsani: “Kodi tiwerenga ciani mu ndime izi zomwe zitiuza kuti Mulungu atikonda ife? Lolani ophunzira alankhuzane pa ndime izi. Atsogolereni pa kuwaonetsa kuti ngakhale Mulungu analenga dziko la kumwamba, ndi dziko lapansi, afunitsitsa kudziwa za cilengedwe ciriconse.

Nenani: “Mu colinga conse ca Mulungu anapempha kuti munthu alamulire pa cilengedwe ciri conse. Cifukwa ici ncoona, ayenera kukonda mtundu uli wonse. Ngati Mulungu atikonda kwambiri, alinso ofunitsitsa kudziwa za umoyo wathu wonse. Pamene ticotsedwa nchito, Mulungu amadziwa. Pamene tadwala amaona, pamene tiri tokha iye asamalira. Palibe comwe ciri cacing’ono kuti sitikhoza kulankhula naye. Coonadi, Mulungu yemwe analenga cilengedwe conse ali ndi mphamvu ya kutithandiza mu bvuto ili yonse. Ngati iye ali ndi mphamvu zonse ndiye kuti akhoza kutithandiza pa bvuto ili yonse.

MUTU 7

MUNTHU AYANG'ANA PA CILENGEDWE CA MULUNGU

COLINGA: Kuphunzira phunziro ili idzandithandiza kuona kuti ndine yani.

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Genesis 26:31; Salmo 8

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Salmo 8

MAU APAMTIMA: “Yehova, Ambuye wathu, Dzina lanu liposadi nanga pa dziko lonse lapansi” (Salmo 8:9)

Munthu wina yemwe anabadwira ku midzi ya m’chigwa ku Kenya, malo omwe anali ouma ndiponso opanda madzi, iye anangodziwa midzi imeneyo kwa zaka zonse 45 za umoyo wace wonse. Izi ndizo zomwe anadziwa.

Tsiku lina analandira kalata kwa mwana wao omwe anali ku sukulu ku Nyeri, mu Kenya. Iye anali kudwala, concu anafuna kuti aonane ndi atate wace. Bambo uja anakonzekera za ulendo. Anacoka pa mudzi nthawi ya masana. Anayenda tsiku lonse ndi usiku wonse.

Pamene kunayamba kuca tsiku lotsatira, basi inali kulowa mu m’zinda wa Nyeri. Pamene bambo uja anayanganitsitsa, anadabwa ndi zomwe anaona. Mitengo itali-itali inagwirira ku maphiri. Kumbali iliyonse ya mscu kunamera mitengo ya masamba (tea ndi coffee). Patsogolo, munthu uja anakhoza kuona Phiri la Kenya. Kaonekedwe ka phiri limeneri kanamukondweretsa. Palibe cinthu cingakhale cacikulu motere ndiponso cabwino!

Pamene analikuseluka mu basi, bambo anafuna kugwa, cifukwa ca misozi m’maso. Mu umoyo wace wonse sanaonepo zinthu zotere! Iye anali atawerenga za mitengo, maphiri ndi mitsinje. Koma kuziona cinali cinthu cina.

Ngati Mulungu akanalenga cilengedwe cabwino coteri, munthu anaganizira, ndiye kuti Mulungu ayenera kuyamikidwa masiku onse.

MULUNGU WATHU WAMKULU

Werengani Salmo 8. Iyi ndi Salmo imodzi yaikulu. Ndi Salmo ya za usiku. Ibvumbulutsa Mulungu mu ulemelero.

Nyimbo iyamba ndi kulira kwa Mulungu yemwe analenga dziko. Ulemerero wa Mulungu ndi waukulu kupambana kumwamba. Palibe yemwe ali wamkulu monga Mulungu. Palibe munthu yemwe ali wamkulu monga Mulungu.

pamodzi, anali kuyimba imeneyi pamodzi. Anayamikira Mulungu kuti ali ndi mphamvu pa dziko lonse.

“Ndime ya 2 itiuza kuti ngakhale ana ang’ono adziwa kuyamikira Mulungu. Kumbukirani pamene yesu analowa mu Yerusalemu pa kuyamba kwa paska? Ana naonso anathandiza kuyamikira kuti “Hosana.” Nthawi zina pamene Yesu anali atatopa kwambiri, ophunzira ace anafuna kuletsa ana kudza kwa iye. Yesu anawaletsa iwo, pakuzindikira kuti anali kulandira cikondi coona kucokera kwa ana.

Funsani: “Ndani adzatifotokozera ndime ya 3?” Lolani m’modzi kapena awiri kufotokoza comwe ndime itanthauza.

Nenani: “ndime 5-8 itifunsa funso lalikulu, kodi funso ili ndi lotani?”

Nenani: “Wolembe analinganiza munthu kucilengedwe conse, ndipo alinganiza Mulungu kwa iye. Adabwitsidwa kuti Mulungu anakonda munthu kopambana kuti anampatsa ulamuliro wolamulira cilengedwe conse. Kodi munafunsapo funso ili? Ndiganiza tonse tinacita. Kodi Mulungu angakonde munthu bwanji yemwe angopitiliza kulephera ndi kucita zoipa? Sitikhoza kumvetsetsa cikondi cimeneco kufikira titadziwa nzeru za Mulungu pamene tikhala naye mu ulemerero.”

Nenani: “Ndime ya 9 itseka nyimbo ndi uthenga wina wa ciyamiko.”

ZOKHUZA KU UMOYO WATHU

Funsani: “Kodi phunziro ili, ili bwanji kwa inu?” Apatseni nthawi yokwanira kuti alankhuzane. Alimbikitseni kuti amasule bwino-bwino za ukulu ulemerero, ndi mphamvu ya Mulungu. Athandizeni kudziwa ciyanjano cao ndi Mulungu.

Nenani: “Nthawi zina munthu amaziganizira kuti ali wamkulu kopambana. Mu America ndi Europe (Maiko a cizungu) muli kupezeka zinthu zatsopano. Nthawi zina zinthu izi zimathandiza munthu. Nthawi zina zimacita zoipa kwa munthu. Kodi mukhoza kuchula zinthu zimenezi zabwino kapena zoipa? Ophunzira akhoza kuchula makhwala, cakudya, zida ndi zina zace. Athandizeni kudziwa zinthu zabwino ndi zoipa.

Ndipo nenani: “Zinthu zonse zomwe munthu amapeza zinaikidwa ndi Mulungu. Munthu anangozipeza cabe. Koma anthu ambiri amene amapeza zinthu zimenezi amaganiza kuti afanana ndi Mulungu koma sitero ai. Tiyenera kuwerenga Salmo imeneyi nthawi zonse ndi kuzifunsa ife tokha.” Ine ndine yani kuti Mulungu andisamalire?

Tsekani mtsonkhano pa kupemphera kuti phunzira akhale ndi nthawi ya ciyamiko sabata lino.

Ndime ya 4-8 ionetsa kuti wolembayo anazikumbukira iye yekha pamene anaimirira ndi Mulungu wace. Anazona kuti anali wamng'ono ndipo wofoka pa ulemerero wa Mulungu. Conco anafunsa: "ncifukwa nciani musamalira munthu wocimwa? Mwaika ulamuliro wonse m'manja ace. Muli ndi ciyanjano ndi munthu kupambana cilengedwe cina ciri conse. M'nampanga ocepa pang'ono kwa angelo. Funso siiyankhidwa ngakhale tsopano. Pokhapo titayamba kugawa ulemerero wa Mulungu muyaya ndi pomwe tikhoza kumvetsetsa cikondi ca Mulungu kwa munthu.

Ndime ya 9 itseka nyimbo, pamene mpingo uyamba kuyamikiranso Mulungu.

KUPHUNZITSA PHUNZIRO

Funsani ophunzira anu kuona ngati pali wina amene anakhoza kuyamikira Mulungu sabata lonse, monga momwe munacitira nthawi yomwe munakomana. Alimbikitseni kunena osati zakupambana kokha, komanso za kulephera kwao kugwiritsa nchito mndandanda wao yakuyamikira Mulungu.

Nenani: "Tiyenera kuphunzira kuyamikira Mulungu. Pamene tidzazindikira ubwino wa Mulungu, tidzakhala okhulupirika kwa iye pa kukhala ndi umoyo wa cigonjetso. Tiyeni tiime tsopano ndi kuyamikira Mulungu. Gwiritsani nchito mindandanda yanu. Ngati simunalipo pamene tinali kulemba mindandanda, onani kwa wina." Kaciwiri, monga mpunzitsi, muyamba ndi pemphero ya ciyamiko. Ndipo lolani ophunzira kuyamika Mulungu. Ayenera kucita bwino tsopano. Alimbikitseni kuti apitirize sabata lonse kuyamikira Mulungu.

Nenani: "Phunziro lathu lero icokera mu Salmo 8. Kumbukirani kuti tinawerenga Salmo ili sabata latha pamene tinali kuphunzira kuyamikira Mulungu. Pali lingaliro lero lakuti titatha maphunziro usiku tione cilengedwe ca Mulungu m'mwamba. Kodi wina anacitapo ici? "Lolani akuuzeni zomwe anaona. Ngati palibe wamene anapita pabwalo kuoana cilengedwe, nenani zomwe munaona. Alimbikitseni kuti akacite ici tsiku lomwe kumwamba kuoneka bwino. Cidzafunika wina kuwerenga pa gawo pomwe panalembedwa "Comwe citanthauza kwa ine" kuwakumbutsa.

KUMASULIRA

Onetsani cithunzi-thunzi comwe mwabweretsa. Nenani: "Mulungu analenga dziko labwino. Anapanga zonse zabwino. Cimo yabweretsa zinthu zoipa mu dziko. Munthu sanasamalire dziko lomwe Mulungu anampatsa. Nthaka ili mu ciopyezo cifukwa ca kulephera kwa munthu. Colinga ca Mulungu cinali ca dziko labwino. Wolemba anadabwitsidwa ndi kukongola komwe anaona. Pemphani wina kuwerenga Salmo 8.

Nenani: "Nyimbo iyi pena inayimbidwa usiku nthawi ya phwando la a Yuda. Anali atafika pa nthawi ya caka catsopano. Pamene mpingo unali kukomana

Kucokera ku milomo ya ana ang'ono Mulungu alandira ciyamiko. Kulira kwao kwa ciyamiko kupanga cipupa coletsa adani a Mulungu. Ici citikumbutsa kuti Mulungu agwiritsa nchito ofoka a pa dziko kukwaniritsa colinga cace.

Mwana wa citsikana yemwe anali ndi zaka zitatu, anauza atate wace, "Mulungu anapanga maluwa abwino." Atate ace sanali Akristu. Cifukwa Mwana ananena ici, iwo anaganiza kwa iwo okha, "Mwana wanga adziwa zambiri za Mulungu kupambana ine." Posacedwa iwo anakhala Akristu cifukwa anafuna kudziwa zambiri za Mulungu.

MALO A MUNTHU M'DZIKO LA MULUNGU

Wolemba Masalmo nthawi ya usiku anali kuyang'ana kumwamba. Iye anadabwa ndi zomwe anaona. Mu Genesis 2:7-19 cirezidwe cinacididwa ndi dzanja la Mulungu. Apa wolemba Salmo 8 akuti kumwamba ndi nchito ya dzala za Mulungu.

Pakuona kukoma kumwamba ndi kumvetsetsa za mlengi, kudziwa kuti ndi wamkulu kopambana, woyimba nyimbo anaganizira za iye yekha. Munthu ndani kuti mumkumbukila? Ndi mwana wa munthu kuti muceza naye? (Salmo 8:4) Iye anali kunena kuti "Kodi ndine yani, kuti Mulungu andisamalire kotere."

Koma tiphunzira kucokera kuwerenga mau ace kuti Mulungu anapanga dzuwa, mwezi ndi nyenyezi. Anapanga zinthu zonse ndi nyama. Ndipo anazipanga kuti tizigwiritse nchito. Munthu ndiwotsiliza kucilengedwe cace ndipo ali wopambana. Sitiyenera kusiya kupembedza Mulungu pa ubwino ndi cikondi cace.

Funso la wolemba Masalmo ndi yofunikira masiku ano. Kodi ndife yani kuti Mulungu atikonde kwambiri? Mulungu anapanga munthu kuti akhale wamng'ono kwa iye.

Pamene Mulungu analenga munthu, anamlenga iye kukhala wamng'ono. Munthu siwabwino ngati Mulungu. Koma Mulungu anapatsa munthu malo a ulemu. Anampatsa mphamvu ya kulamulira pa cilengedwe cace conse. Mulungu akonda munthu kwambiri.

MOMWE MUNTHU ANAGWIRITSIRA NCHITO DZIKO LA MULUNGU

Mulungu anapatsa munthu mphamvu kulamulira zinthu zonse zomwe iye analenga. Anamuza kugwiritsa nchito zinthu zonse zomwe iye analenga. Koma azigwiritse mwa nzeru ndi munjira yabwino. Munthu adzanenera pamaso pa Mulungu momwe anagwiritsira cilengedwe ca Mulungu.

Wolemba Salmo 8 ayamikira Mulungu kaciwiri mu ndime ya 9. Mmulungu afunika kutamandidwa.R

COMWE CITANTHAUZA KWA INE

Sankhani tsiku sabata lino ndipo muturuke panja. Pezani malo pomwe mukhoza kuona kumwamba bwino-bwino. Gonani pansi pamene maso anu ayang'ana kumwamba. Pamene muli cigonere yamikirani Mulungu cifukwa ca ukulu wace womwe umalenga zonse zabwino. Ganizirani za ukulu wace, ulemerero wace ndi mphamvu ndipo ganizirani za inu nokha. Ganizirani monga momwe wa Masalmo anacitira kuzindikira kuti muli ochepa kupambana Mulungu. Kodi maganizo otere anakudabwitsani kuti Mulungu wotere akonda inu? Kapena mudzamuyamika pamene mugona kuti anakukondani kwambiri ndi kukutumizirani Mwana wace kudzafera macimo anu?

Mulungu analenga zinthu zonse, ndipo zinali zabwino. Munthu ndi wopambana cilengedwe conse. Mulungu anapatsa munthu nchito ya kulamulira zilengedwe zina mwa nzeru.

Munthu ayenera kumvera Mulungu. Ayenera kugwira nchito yace bwino yomwe anapatsidwa.

Kodi mwalandira nchito yomwe Mulungu anakupatsani kusamalira zilengedwe zace? Kodi muli kugwiritsa nchito zilengedwe zace mwa nzeru?

MUTU 7

KWA MPHUNZITSI

MUNTHU AYANG'ANA PA CILENGEDWE CA MULUNGU

KUPHUNZIRA KOYAMBA: Genesis 1:26-31; Salmo 8

NDIME ZA MPHUNZIRO LA LERO: Ahebri 13:1-8, 20-21

COONADI: Ngakhale kuti Mulungu ndi woyera ndipo wamphamvu, akonda munthu ndipo afuna kuti abwere kwa iye.

COLINGA CAKUPHUNZITSA

Ndifuna ophunzira kuona mphamvu ya Mulungu.

ZOTHANDIZIRA PAKUPHUNZITSA

Ngati mukwaniritsa, bweretsani cithunzi-thunzi ca mwezi ndi nyenyezi kapena maluwa, tsamba, zipatso zakucha (zakupya), kapena ndiwo.

KUKONZEKERA KUPHUNZITSA

KUPHUNZIRA KOYAMBA

Salmo 8 ndi yodziwika kwambiri. Yobu 7:17 anena, "Munthu ndani kuti mumkuze." Salmo 144:3 afunsa, Yehova, munthu ndani kuti mumdziwa? Mateyu 21:16 anena, "...ndipo Yesu ananena kwa iwo, inde simunawerenga kodi, mkamwa mwa makanda ndi oyamwa munafotokozera zolemekeza? Ahebri 2:6-7 anena, "....munthu ndani kuti mumsamalire iye? Kapena mwana wa munthu kuti muceza naye? Munamcepsa pang'ono ndi angelo, mudambveka iye korona wa ulemerero ndi ulemu."

Salmo 8:1 iyamba ndi ciyamiko kwa Mulungu. Dzina lace ndi lalikulu padziko lonse. Dzina lace litanthauza Ambuye Mulungu. Ulemerero wace ndi waukulu kwambiri.

Ndime ya 2 inena za ana ang'ono omwe akhoza kuzindikira nzeru ndi kukoma kumene Mulungu analenga. Tanthauzo lina la ndime iyi ndi lakuti ana ang'ono ayamikira cilengedwe ca Mulungu, comwe ciri cipupa cocinjiriza adani a Mulungu.

Mu ndime ya 3, wolemba adabwitsidwa ndi nchito ya Mulungu pa kulenga kumwamba. Nyenyezi, mwezi nzokongola.